(CHICHEWA)

# Manong'onong'o a Satana ndi Machiritso ake




Shaykh-e-Tariqat, Ameer-e-Ahl-e-Sunnat
Muyambitsi wa Dawat-e-Islami, Allamah Maulana Abu Bilal

**MUHAMMAD ILYAS**

Attar Qadiri Razavi



Linamasuliridwa Machichewa ndi Nthambi Yomasulira ya Dawat-e-Islami

وَسوَسے اور اُن کا عِلاج

Waswasay aur Un ka ‘Ilaj

# MANONG'ONONG'O A SATANA NDI MACHIRITSO AKE

Kabukuka kanalembedwa ndi Shaykh-e-Tareeqat, Ameer-e-Ahl-e-Sunnat, muyambitsi wa Dawat-e-Islami ‘Allamah Maulana Abu Bilal Muhammad Ilyas Attar Qaadiri Razavi دَامَتْ بَرَكَاتُهُمُ الْعَالِيَه mu chiyankhulo Cha Urdu. **Nthambi Yomasulira** (Dawat-e-Islami) yamasulira mu Chichewa. Ngati mungapeze cholakwika chilichonse pomasulira kapena pakulemba, chonde dziwitsani nthambi yomasulira pa Keyala kapena imelo ili m’musiyi ndi cholinga chopeza malipiro [sawab].

**Nthambi Yomasulira ya (Dawat-e-Islami)**

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah, Mahallah Saudagran, Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

**UAN:** ☎ +92-21-111-25-26-92 – Ext. 7213

**Imelo:** 🖃 translation@dawateislami.net

**MANONG'ONONG'O A SATANA NDI MACHIRITSO AKE**

Kumasulira kwa m' Waswasay aur Un ka 'Ilaj'

MAWUMWINI ONSE NDI OTETEZEDWA

Umwini © 2025 Maktaba-tul-Madinah

Palibe gawo lililonse la kusindikiza uku lomwe litha kutulutsidwa, kapena kutumizidwa, m'mawonekedwe aliwonse kapena mwanjira iliyonse, zamagetsi, zamakina, kujambula, kujambula mu mawu kapena mwanjira ina iliyonse, popanda chilolezo cholembedwa cha Maktaba-tul-Madinah.

**Kusindikiza kwachinayi:** Jumādil Šānī, 1447 AH – (Dec, 2025)
**Lamasuliridwa ndi:** Nthambi yomasulira (Dawat-e-Islami)
**Wosindikiza:** Maktaba-tul-Madinah
**Kuchuluka:** -

## THANDIZO

Chonde khalani omasuka kulumikizana nafe ngati mukufuna kuthandiza pa kusindikiza kwa buku lililonse lachipembedzo kapena kabuku pofuna kutumiza thawāb kwa anthu omwe anamwalira am'banja mwanu.

**Maktaba-tul-Madinah**

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah Mahallah Saudagran,
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

✍ **Imelol:** global@maktabatulmadinah.com | feedback@maktabatulmadinah.com
✆ **Foni:** +92-21-34921389-93
💻 **Webusayiti:** www.dawateislami.net | www.maktabatulmadinah.com

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ رَبِّ الْعٰلَمِيْنَ وَ الصَّلٰوةُ وَ السَّلَامُ عَلٰى خَاتَمِ النَّبِيّٖنَ

اَمَّا بَعْدُ فَاَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْمِ بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ

# Du'a Powerenga Buku

Werengani Du'a (pempho) musanawerenge buku lachipembedzo kapena musanayambe phunziro lachisilamu; mudzakumbukira china chilichonse mwaphunzira, اِنْ شَآءَاللّٰه:

اَللّٰهُمَّ افْتَحْ عَلَيْنَا حِكْمَتَكَ وَانْشُرْ

عَلَيْنَا رَحْمَتَكَ يَا ذَا الْجَلَالِ وَالْاِكْرَام

## Kumasulira

E Allah عَزَّوَجَلَّ! Titsegulireni makomo a maphunziro komanso a luntha ndipo tichitireni chisoni! E inu omwe muli wolemekezeka kwambiri komanso Wawulemerero!

*(Al-Mustatraf, buku. 1, tsamba. 40)*

**Dziwani:**

Nfunireni zabwino Ntumiki (Salat-'Alan-Nabi) صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَسَلَّم kamodzi musanayambe komanso kumapeto kwa Du'a.

# ZANKATIMU


**MANONG'ONONG'O A SATANA** ............................................1

**NDI MACHIRITSO AKE**..........................................................1

Kunfunira Zabwino Mtumiki (Salat-'Alan-Nabi) pambuyo pa Du'a ya Qunoot ndi zopambana ..............................................1

Kumasulira mchichewa kwa 'وَسوَسہ' [Waswasah]..............................2

Aliyense amatsagana ndi mngelo ndi Satana ..................................3

Kodi ndani amatchedwa ﴿هَمزاد﴾ [Hamzad]? ................................5

Hamzad wa Mtumiki Woyera analowa Chisilamu ..........................5

Aliyense amatsagana ndi Satana ....................................................6

Satana ali nfulu koma iwe uli otanganidwa....................................6

Satana amayenda m'thupi ngati magazi..........................................7

Mavuto 6 aakulu a kudya kwambiri ................................................8

Njira zosiyanasiyana za manong'onong'o a satana........................10

Manong'onong'o a satana okhudza Allah عَزَّوَجَلَّ..............................12

Sikuti funso lililonse limayankhidwa ............................................12

Machiritso a Quran a manong'onong'o a satana ...........................13

Imam Raazi ndi Satana...................................................................14

Manong'onong'o a satana okhudza tsogolo (chikonzero).............16

Zomwe wina adzachite zinalembedwa kale m'chikonzero...........16

Fatwa yofunika yokhudza tsogolo (chikonzero) ...........................17

Machiritso abwino a manong'onong'o a satana okhudza tsogolo19

Manong'onong'o a satana okhudza chikhulupiriro .......................21

Manong'onong'o owopsa a satana.................................................22

Palibe chilango pa manong'onong'o a satana................................22

Kuthekera kwa chilango pa manong'onong'o a satana..................23
Chikhulupiriro sichiwonongedwa ndi manong'onong'o a satana24
Kuwona manong'onong'o a satana ngati oyipa ndi chikhulupiriro chenicheni...........................................................................24
Manong'onong'o a satana pa nthawi ya kulambira........................26
Mayina a Asatana 9 ndi ntchito zawo .............................................26
Manong'onong'o a satana M'mizikiti.............................................28
Manong'onong'o a satana pa nthawi ya Ghusl ...............................30
Choyambitsa manong'onong'o a satana pa nthawi ya Ghusl........30
Kufotokozera kwa Hadees yomwe yatchulidwa pamwambapa....31
Fanizo lonena za vuto loyambitsidwa ndi manong'onong'o a satana ...............................................................................................32
Manong'onong'o a satana pa nthawi ya Wudu..............................34
Kuwaza madzi pa gawo la thalawuza .............................................34
Zoyenera kuchita ngati wina akumana ndi manong'onong'o a satana pa nthawi ya Wudu?...........................................................35
Manong'onong'o a satana okhudza kuwonongeka kwa Wudu pa nthawi ya Salah.............................................................................36
Nena kwa Satana 'ndiwe wabodza' .................................................37
Ine komanso ntchito yanga si ife angwiro......................................37
Kanani manong'onong'o a satana..................................................39
Manong'onong'o a satana pa nthawi ya Salah................................39
Njira yopewera manong'onong'o a satana pa nthawi ya Salah.....40
Malovu amagwera n'kamwa mwa Satana.......................................41
Manong'onong'o a satana okhudza chiwerengero cha ma Rak'aat mu Salah ..........................................................................................42

Lamulo lokhudza kukayikira pa chiwerengero cha ma Rak'aat mu Salah....43
Kunyozeka kwa Satana....44
Woyera ntima anakwiyitsa Satana....45
Njira yapadera yokanira manong'onong'o a satana....46
Ndinthu musapereke chidwi ku manong'onong'o a satana....47
Manong'onong'o a satana okhudza ukhondo....48
Palibe chifukwa chofufuzira zokhudza nyansi....48
Mfundo za Madani zokhudza zotsalira za nyama....49
Machiritso odabwitsa a manong'onong'o a satana kudzera mu matope....52
Matope ndi oyera pokhapokha wina atatsimikiza kuti ndi onyansa....52
Kodi ngodya iti ya nsalu yoti iyeretsedwe?....53
Kodi chidzachitike ndi chani mwana akayika dzanja lake m'madzi ?....54
Manong'onong'o a satana okhudza chisudzulo....54
Kufunsa za chakudya kungatsegule chitseko cha machimo....56
Mitundu iwiri ya Satana....58
Asatana m'mawonekedwe a munthu....59
MACHIRITSO A MANONG'ONONG'O A SATANA....63
Satana m'mawonekedwe a chule....63
Mtumiki Woyera nthawi zonse ankamukumbukira Allah عَزَّوَجَلَّ....64
Satana – wofowoka ngati mpheta....64
Satana amachoka....65
Nkhondo pakati pa Zikr ndi manong'onong'o a satana....65

Satana amadya ntima......................................................................66
Kusalapa ngakhale mutakwanitsa zaka 40......................................66
Musapereke chidwi ku manong'onong'o a satana...........................67
Machiritso 8 a manong'onong'o a satana .......................................69
Zoyenera kuchita ngati manong'onong'o a satana sakutha?.........71
Kumukumbukira Mulungu kumamupweteka Satana ...................73
Mfundo za Madani ........................................................................77
Maganizo a kusakhulupirira m'maganizo ......................................77

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ رَبِّ الْعٰلَمِیْنَ وَالصَّلٰوةُ وَالسَّلَامُ عَلٰی خَاتَمِ النَّبِیّٖن

اَمَّا بَعْدُ فَاَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّیْطٰنِ الرَّجِیْمِ بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِیْمِ

# MANONG'ONONG'O A SATANA

## NDI MACHIRITSO AKE

Ngakhale Satana ayesetse kukupangitsani ulesi motani, werengani kabukuka kuyambira pachiyambi mpaka pamapeto. Mudzatetezedwa ku zotsatira zowopsa za manong'onong'o a satana اِنْ شَآءَاللّٰه عَزَّوَجَلَّ.

### Kunfunira Zabwino Mtumiki (Salat-'Alan-Nabi) pambuyo pa Du'a ya Qunoot ndi zopambana

Sayyiduna Abu Haleemah Mu'aaz رضی اللّٰہ عنہ ankamufunira zabwino Mtumiki ﷺ (Salat-'Alan-Nabi) pamodzi ndi Du'a ya Qunoot. *(Fadl-us-Salat-'Alan-Nabi lil Qadi Al-Jahdami, tsamba. 87, Raqm 89)*

Katswiri wodziwika komanso wotsogola wa Shari'ah ndi Tareeqah, 'Allamah Maulana Mufti Muhammad Amjad 'Ali A'zami رحمۃ اللّٰہ علیہ anafotokoza pa tsamba 655 la buku loyamba la masamba 1250 la Bahar-e-Shari'at losindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah, nthambi yosindikiza ya Dawat-e-Islami: Ndibwino kumufunira zabwino Mtumiki (Salat-'Alan-Nabi) pambuyo pa Du'a ya Qunoot (mu Rak'at yachitatu ya Salat-ul-Witr).

صَلُّوْا عَلَی الْحَبِیْب صَلَّی اللّٰهُ عَلٰی مُحَمَّد

## Kumasulira mchichewa kwa 'وَسوَسہ' [Waswasah]

Abale anga wokondedwa achisilamu! Mawu akuti ﴿وَسوَسہ﴾ [Waswasah] kwenikweni amatanthawuza 'kunong'oneza'. Malinga ndi Shari'ah, 'Waswasah' amatanthawuza maganizo oyipa ndi malingaliro. *(Ashi'ah, buku. 1, tsamba. 300)*

Zanenedwa m'buku la 'Tafseer Baghawi': 'Waswasah' ndi lingaliro limene Satana amayika mu ntima mwa munthu.

*(Tafseer Baghawi, buku. 2, 4, tsamba. 127, 518)*

Nthawi zambiri, aliyense amakumana ndi manong'onong'o a satana. Wina amakumana nawo kwambiri ndipo wina pang'ono. Anthu ena omwe ali ndi nkhawa kwambiri amapitiriza kuganizira za manong'onong'o a satana ndipo amakumana ndi mavuto. Ngati anyalanyazidwa, manong'onong'o a satana nthawi zambiri amatha. Mukangoyamba kumva manong'onong'o a satana, yambani kukumbukira Allah عَزَّوَجَلَّ. Mwachitsanzo, yambani kunena 'Allah, Allah'. Satana adzathawa اِنْ شَآءَاللّٰہ عَزَّوَجَلَّ. Msilamu akamapembedza kwambiri Allah عَزَّوَجَلَّ m'pamene Satana amamutsutsa kwambiri, kusonyeza udani wake. Poyika mitundu yosiyanasiyana ya misampha yachinyengo, Satana amayesetsa momwe angathere kuti amulepheretse kupembedza Allah عَزَّوَجَلَّ ndi kutsatira Sunnah ya Mtumiki Wake Wokondedwa ndi Wodalitsika صَلَّى اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم. Satana amapitiriza kumusokoneza poyika mitundu yosiyanasiyana ya maganizo



www.dawateislami.net

onyansa ndi oyipaa m'maganizo mwake. Nthawi zina, munthu amagwa mumsampha wa manong'onong'o a satana mosadziwa, n'kusiya ntchito yabwino ndi yaumulungu. Motero Satana amakhala wapambana pa ntchito yake. Allah عَزَّوَجَلَّ anawuza Mtumiki Wake Wokondedwa صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم mu Vesi 97 ndi 98 ya Surah Al-Mu'minoon ya gawo 18:

وَ قُلۡ رَّبِّ اَعُوۡذُ بِکَ مِنۡ ہَمَزٰتِ

الشَّیٰطِیۡنِ ﴿۹۷﴾ وَ اَعُوۡذُ بِکَ رَبِّ اَنۡ یَّحۡضُرُوۡنِ ﴿۹۸﴾

*Ndipo nena, 'E, Mbuye wanga! Ndikupempha chitetezo Chanu ku manong'onong'o a ziwanda. Ndipo Mbuye wanga, ndikupempha chitetezo Chanu kuti asabwere kwa ine.'*

*[Kanz-ul-Iman (Kutanthauzira kwa Quran)] (Gawo 18, Al-Mu`minoon, Vesi 97, 98)*

*Na waswasay aayain na kabhi ganday khayalat*

*Ho zihn ka aur dil ka 'ata Qufl-e-Madinah*

*Kumasulira: Ndisakhale ndi manong'onong'o a satana kapena maganizo onyansa!*

*Ndithe kudalitsidwa ndi Qufl-e-Madinah ya malingaliro anga ndi ntima wanga!*

## Aliyense amatsagana ndi mngelo ndi Satana

Ichi ndi chidule cha mawu a Sayyiduna Imam Muhammad Bin

Muhammad Bin Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ochokera pa tsamba 79 ndi 80 la buku la masamba 344 ﴿مِنهَاجُ الْعَابِدِيْن﴾ [Minhaj-ul-'Aabideen] losindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah, nthambi yomasulira ya Dawat-e-Islami: Allah عَزَّوَجَلَّ wayika mngelo pa ntima pa munthu aliyense. Mngeloyo amapitiriza kumuyitanira ku zabwino. Mngelo ameneyu amatchedwa ﴿مُلْهِم﴾ [Mulhim] ndipo kuyitana kwake kumatchedwa ﴿اِلْهَام﴾ [Ilhaam]. Mbali inayi, Satana nayenso amayikidwa ndi Allah عَزَّوَجَلَّ. Satana uyu amamuyitanira ku zoyipa. Satana amatchedwa ﴿وَسْوَاس﴾ [Waswaas] ndipo kuyitana kwake kumatchedwa ﴿وَسْوَسَه﴾ [Waswasah].

Sayyiduna Imam Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anafotokozanso kuti: Ngakhale akatswiri ambiri a Chisilamu رَحِمَهُمُ اللّٰه ali ndi maganizo akuti mngelo amayitanira anthu ku zabwino zokha ndipo Satana ku zoyipa zokha, komabe mtsogoleri wanga wawuzimu ananena kuti Satana nthawi zina amapangitsa anthu kuchita zoyipa ngakhale powayitanira ku zabwino. Amachita izi powayitanira ku ntchito yaying'ono yabwino m'malo mwa yayikulu kapena amawapangitsa kuchita tchimo lalikulu lomwe ndi loyipitsitsa kuposa mphotho ya ntchito yabwino. Mwachitsanzo, ngati munthu wachita ntchito yabwino, Satana amamupangitsa iye kukhala 'wokhutira'.

*Sarwar-e-Deen li-jiye apnay natuwano" ki khabar*

*Nafs-o-Shaytan Sayyida kab tak dabatay jayain gey*

*Kumasulira: O Nfumu ya chipembedzo (صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم)! Chonde samalirani akapolo anu ofowoka. Kodi Nafs ndi Satana adzapitiriza kutipondereza mpaka liti? (Hadaiq-e-Bakhshish)*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Kodi ndani amatchedwa ﴿هَمزاد﴾ [Hamzad]?

Zimanenedwa m'mabuku a ﴿مِرْقَاة﴾ [Mirqat] ndi ﴿اَشِعَّةُ اللَّمْعَات﴾ [Ashi'a-tul-Lam'aat] kuti mwana wa munthu akangobadwa, mwana wa Satana nayenso amabadwa. Mwana wa Satana amatchedwa ﴿هَمْزَاد﴾ Hamzaad] m'Chipeshayani ndi ﴿وَسْوَاس﴾ [Waswas] m'Chiyarabu. *(Ashi'a-tul-Lam'aat, buku. 1, tsamba. 87; Mirqat, buku. 1, tsamba. 244; Mirat, buku. 1, tsamba. 83)*

## Hamzad wa Mtumiki Woyera analowa Chisilamu

Sayyiduna 'Abdullah Bin Masood رَضِیَ اللّٰہُ عَنْهُ ananena kuti Mtumiki Wolemekezeka komanso Wodziwika صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Aliyense wa inu amatsagana kapena amayenda limozi ndi jini (mwachitsanzo, Satana) komanso mngelo.' Anthu anafunsa, 'Ya Rasoolallah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ! Ngakhale inu?' Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Ngakhale ine ndimatsagana naye koma Allah عَزَّوَجَلَّ

anandithandiza polimbana naye, kumupanga kukhala Msilamu. Tsopano amandipatsa malingaliro okhudza zabwino zokha.' *(Sahih Muslim, tsamba. 1512, Hadees 2814)*

## Aliyense amatsagana ndi Satana

Abale achisilamu okondedwa! Kumbukirani kuti Satana wotsagana ndi Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم yekha ndi amene anakhala Msilamu. Satana otsagana ndi anthu ena onse ndi osakhulupirira olimba [mukunena kwina, ndi amphanvu]. Komabe, Satana yemwe ndi wosakhulupirira wolimba amayikidwa kuti azinong'oneza m'mitima yathu ndipo amapitiriza kutitsutsa nthawi zonse, kusonyeza udani wake kwa ife.

*Mujhay Nafs-e-zalim pay ker di-jiye ghalib*

*Ho nakaam hamzad Ya Ghaus-e-A'zam*

*Kumasulira: O Ghaus-e-A'zam! Ndipangitseni kulamulira Nafs mwankhanza. Satana wanga wotsagana nane alephere!*

*(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 297)*

## Satana ali nfulu koma iwe uli otanganidwa

Potchula mawu a Sayyiduna Yahya Bin Mu'aaz Raazi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه, Hujjat-ul-Islam, Sayyiduna Imam Muhammad Bin Muhammad Bin Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anafotokoza pa tsamba 77 la buku lomasuliridwa m'Chiurdu la masamba 344 la Minhaj-ul-

'Aabideen losindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah, nthambi yomasulira ya Dawat-e-Islami: Satana ali mfulu koma iwe uli otanganidwa. Amakuyang'ana koma iwe sungathe kumuwona. Iwe wamuyiwala koma iye sanakuyiwale. Ngakhale nkati mwako muli abwenzi ndi othandizira ambiri a Satana (monga Nafs ndi zilakolako ndi zina zambiri). Choncho, ndikofunikira kulimbana ndi Satana ndikumugonjetsa. Kupanda kutero, sungathe kukhala otetezeka ku zoyipa ndi mavuto a Satana. *(Minhaj-ul- 'Aabideen – (Chiarabu), tsamba. 46)*

*Kalayjah shayateen ka tharra uthay ga*

*Pukaro sabhi mil kay 'Ya Ghaus-e-A'zam'*

*Kumasulira: Itanani 'Ya Ghaus-e-A'zam' nonse pamodzi. Asatana adzanjenjemera ndi mantha.*

*(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 296)*

صَلُّوْا عَلَی الْحَبِیْب صَلَّی اللّٰہُ عَلٰی مُحَمَّد

## Satana amayenda m'thupi ngati magazi

Satana ali pafupi kwambiri ndi aliyense wa ife. Mtumiki Wolemekezeka ndi Wodziwika صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati, 'Mosakayika, Satana amayenda m'thupi la munthu ngati magazi.' *(Sahih Bukhari, buku. 1, tsamba. 669, Hadees 2038)*

Ma Sufi akuluakulu رَحِمَهُمُ اللّٰه anati: Choncho tsekani njira za

Satana pogwiritsa ntchito njira ya njala. *(Kashf-ul-Khifa, buku. 1, tsamba. 198)*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Mavuto 6 aakulu a kudya kwambiri

Amene amadya kwambiri ayenera kuganizira momwe angachotsere Satana. Hujjat-ul-Islam, Sayyiduna Imam Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati: Zimanenedwa kuti kudya kwambiri kumayambitsa zoyipa zisanu ndi chimodzi:

1. Palibenso mantha a Mulungu muntima.
2. Palibe chifundo kwa ena chifukwa amene amadya kwambiri amaganiza kuti aliyense ali ngati iwo ndipo motero samakhala ndi chifundo kwa ena.
3. Kupembedza kumawoneka ngati chiphinjo.
4. Kufewa sikumabwera muntima ponvetsera malangizo ndi (mawu olimbikitsa a Sunnah).
5. Ngati munthu wodya kwambiri ali mlaliki ndipo amapereka maulaliki, kuwuza ena mawu anzeru, sizimakhudza mitima ya anthu.
6. Mitundu yosiyanasiyana ya matenda imayambika.

*(Chidule chochokera ku: Ihya-ul-'Uloom, buku. 3, tsamba. 40)*



www.dawateislami.net

*Ya Ilahi bhook ki dawlat say mala maal ker*

*Dau jahan mayn apni Rahmat say mujhay khush-hal ker*

*Kumasulira: O Wamphanvu zonse! Ndidalitseni ndi chuma chanjala. Ndipangitseni kukhala wolemera m'moyo wapadziko lapansi komanso m'moyo womwe ulinkudza mwa chisomo chanu.*

(Kuti muphunzire zambiri za ubwino wa njala ndi kuyipa kwa kudya kwambiri, werengani 'Ubwino wa Njala' – mutu umene ukupezeka mu Faizan-e-Sunnat buku 1.)

Pamene Allah عَزَّوَجَلَّ anatemberera Satana, Satana analengeza udani kwa munthu. Zimene Satana ananena zatchulidwa mu Vesi 16 ndi 17 za Surah Al-A'raf mu gawo 8:

قَالَ فَبِمَاۤ اَغْوَیْتَنِیْ لَاَقْعُدَنَّ لَهُمْ صِرَاطَكَ الْمُسْتَقِیْمَ ﴿۱۶﴾ ثُمَّ لَاٰتِیَنَّهُمْ مِّنْۢ بَیْنِ اَیْدِیْهِمْ وَ مِنْ خَلْفِهِمْ وَ عَنْ اَیْمَانِهِمْ وَ عَنْ شَمَآىٕلِهِمْؕ وَ لَا تَجِدُ اَكْثَرَهُمْ شٰكِرِیْنَ ﴿۱۷﴾

*Anati, 'Chifukwa chake ndikulumbira kuti popeza mwandipanga kukhala osochera, ndithudi ndidzawadikira pa Njira Yanu Yowongoka. Kenako ndithudi ndidzabwera kwa iwo – kuchokera kutsogolo kwawo ndi kuchokera kumbuyo kwawo ndi kuchokera kumanja kwawo ndi kuchokera kumanzere kwawo; ndipo simudzapeza ambiri a iwo ali othokoza.'*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 8, Al-A'raf, Vesi 16, 17)*

*Mahboob-e-Khuda sar pay ajal aa kay khari hay*

*Shaytan say 'Attar ka Iman bacha lo*

*Kumasulira: O Mtumiki Wokondedwa* صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم*! Imfa yanga yayandikira. Chonde tetezani chikhulupiriro cha 'Attar kwa Satana.* (Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 86)

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Njira zosiyanasiyana za manong'onong'o a satana

Abale okondedwa achisilamu! Satana ndi m'dani ngakhale wa abwenzi ake apantima omwe alibe udani naye. Osakhulupirira, opotoka, olakwa ndi ochimwa samamutsutsa Satana koma amamunvera. Ngakhale zili choncho Satana sawasiya ndipo amapitiriza kunong'oneza m'mitima mwawo, kuwapanga kukhala owuma ntima kwambiri ndikuwayandikitsa ku chiwonongeko. Tsopano taganizirani udani wowawa umene Satana adzakhala nawo kwa akatswiri a Chisilamu ndi alaliki a Sunnah ﴿كَثَّرَهُمُ اللهُ الْمُبِيْن﴾ [mukunena kwina, Allah عَزَّوَجَلَّ achulukitse anthu oterowo] amene nthawi zonse amamutsutsa ndi kumukwiyitsa powadziwitsa Asilamu za kuwukira kwake, motero kuwononga maganizo ake osokoneza. Tiyenera kupempha chitetezo cha Allah عَزَّوَجَلَّ nthawi zonse ku manong'onong'o a Satana chifukwa wotembereredwayu ndi wanzeru kwambiri komanso wochenjera. Amayambitsa

manong'onong'o mu ntima mwa aliyense malingana ndi maganizo ake.

Wothirira ndemanga wodziwika, woganiza mozama wa Ummah, Mufti Ahmad Yar Khan رحمۃ اللّٰہ علیہ ananena kuti, 'Kumbukirani! Satana amayambitsa manong'onong'o awumaphunziro m'mitima mwa akatswiri ophunzira, manong'onong'o opembedza m'mitima mwa a Sufi ndi manong'onong'o wamba m'mitima mwa anthu wamba. Ndiye kuti, amaponya ukonde wosiyana kuti agwire munthu wosiyana. Nthawi zambiri, (Satana amawapanga machimo kukhala okongola kwambiri moti) munthu amachita tchimo, poganiza kuti ndi ntchito yopembedzeka.' *(Mirat-ul-Manajih, buku. 1, tsamba. 87)*

Nthawi zina, Satana amawonekera pamaso pa munthu ndikudzitcha kuti ndi Wamphanvu zonse, kuyesa kusokoneza munthuyo. Anachita izi pamene adawonekera pamaso pa Mfumu ya Baghdad, chisomo chake Ghaus-e-A'zam, Sayyiduna Shaykh 'Abdul Qaadir Jeelani قُدِّسَ سِرُّہُ الرَّبَّانِی.

*Sun lo Shaytan nay her taraf her su*

*Khoob phayla kay jaal rakha hay*

*Kumasulira: Invani! Satana wafalitsa ukonde wake kutali ndi ponseponse m'njira zonse.*

صَلُّوْا عَلَی الْحَبِیْب     صَلَّی اللّٰہُ عَلٰی مُحَمَّد



www.dawateislami.net

## Manong'onong'o a satana okhudza Allah عَزَّوَجَلَّ

Mtumiki Wokondedwa koimanso Wodalitsika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: Satana amabwera kwa aliyense wa inu ndipo amati, 'Ndani analenga chinthu ichi ndi ichi?' Satana amanenanso kuti, 'Ndani analenga Mbuye wanu?' Akakusokonezani mpaka pamlingo umenewu, nenani ﴿اَعُوْذُ بِاللّٰهِ﴾ ndi kuzitchinjiriza kwa Allah kuzimenezi.

*(Sahih Bukhari, buku. 2, tsamba. 399, Hadees 3276)*

## Sikuti funso lililonse limayankhidwa

Poyankhula pa Hadees yomwe yatchulidwa, wothirira ndemanga wodziwika, woganiza mozama wa Ummah, Mufti Ahmad Yar Khan رحمۃ اللّٰہِ علیہ anafotokoza kuti: Musayesere n'komwe kuganizira za yankho la manong'onong'o a satanawa. Kupanda kutero, Satana adzafunsa funso lina. Muthamangitseni ponena kuti ﴿اَعُوْذُ بِاللّٰهِ﴾.

Sikuti funso lililonse limayankhidwa. Pamene Satana sanagwade pamaso pa Sayyiduna Aadam عَلٰی نَبِیِّنَا وَعَلَیْهِ الصَّلٰوۃُ وَالسَّلَام ndipo anapereka zifukwa zake, Allah عَزَّوَجَلَّ sanaziyankhe zifukwazo. M'malo mwake, Allah عَزَّوَجَلَّ anati ﴿فَاخْرُجْ مِنْهَا﴾ (kumasulira kuti, tuluka Kumwamba).[1] Kumbukirani kuti

[1] Gawo 14, Surah Al-Hajar, Vesi 34

kunena ﴿اَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْمِ﴾ ndi pemphero lamphanvu kwambiri komanso lothandiza kuthamangitsa Satana.

*(Mirat-ul-Manajih, buku. 1, tsamba. 82)*

*Nafs-o-Shaytan ki shararat door ho*

*Yeh karam Ya Mustafa farmaiye*

*Kumasulira: O Mtumiki Wokondedwa Mustafa* صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم *! Chonde ndidalitseni ndi chisomo chanu mwa kunditeteza ku zoyipa za Nafs ndi Satana.*

*(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 87)*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب      صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Machiritso a Quran a manong'onong'o a satana

Abale achisilamu okondedwa! Zakhala zowonekeratu kuti munthu ayenera kuchotsa manong'onong'o a satana powerenga mawu oti ﴿اَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْمِ﴾ Qur'an Yopatulika yalamulanso kuti munthu apemphe chitetezo cha Allah عَزَّوَجَلَّ ngati akukumana ndi manong'onong'o a satana. Zanenedwa mu Vesi 200 ya Surah Al-A'raf mu gawo 9:

وَ اِمَّا يَنْزَغَنَّكَ مِنَ الشَّيْطٰنِ

نَزْغٌ فَاسْتَعِذْ بِاللّٰهِ ؕ اِنَّهٗ سَمِيْعٌ عَلِيْمٌ ﴿۲۰۰﴾

*Ndipo iwe wonvetsera! Ngati manong'onong'o aliwonse ochokera kwa satana akukuvutitsa, pempha chitetezo cha Allah; ndithudi Iye Ngwakunva Zonse, Ngodziwa Zonse.*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 9, Surah Al-A'raf, Vesi 200)*

*Mujh ko day day panah shaytan say*

*Is say Iman mayra bacha Ya Rab*

*Kumasulira: O Wamphanvu zonse! Ndipatseni chitetezo kwa Satana. Tetezani chikhulupiriro changa kwa iye.*

## Imam Raazi ndi Satana

Zanenedwa pa tsamba 493 ndi 494 la buku la masamba 502 lotchedwa Malfuzaat-e-A'la Hadrat [Malangizo ochokera kwa A'la Hadrat] losindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah, nthambi yomasulira ya Dawat-e-Islami: Nthawi yomwe (Sayyiduna) Imam Fakhruddin Raazi رحمۃ اللہ علیہ ankamwalira, Satana anawonekera. Panthawiyo, Satana amayesetsa kwambiri kuti munthu womwalirayo ataye chikhulupiriro chake chifukwa amadziwa kuti munthu womwalirayo sadzapezanso chikhulupiriro ngati atasokera panthawiyi. Choncho, Satana anamufunsa Sayyiduna Imam Fakhruddin Raazi رحمۃ اللہ علیہ, 'Wakhala moyo wako wonse ukukangana ndi kukambirana. Kodi ukumudziwa Wamphanvu zonse?' Imam Raazi رحمۃ اللہ علیہ anati, 'Mosakayika, Wamphanvu Zonse ndi Mmodzi.' 'Umboni uliwonse,' anafunsa Satana. Iye رحمۃ اللہ علیہ anapereka umboni

koma Satana wotembereredwa, mphunzitsi wakale wa angelo, anayankha mochenjera. Imam Raazi رحمۃُ اللّٰہِ علیہ anapereka umboni wina koma Satana anayankhanso. Sayyiduna Imam Raazi رحمۃُ اللّٰہِ علیہ anapereka ngakhale mawumboni 360 koma onse anayankhidwa ndi Satana. Tsopano Imam anali ndi nkhawa kwambiri ndipo anakhumudwa. Mtsogoleri wake wa uzimu (Sayyiduna Shaykh) Najmuddin Kubra رضی اللّٰہ عنہ anali akuchita Wuzu kumalo akutali. Iye anamuyitana Imam Raazi رحمۃُ اللّٰہِ علیہ kuchokera kumalo omwewo, 'Bwanji siwunanene kuti ndimakhulupirira umodzi wa Wamphanvu zonse popanda umboni uliwonse?'

Abale achisilamu okondedwa! Kodi mwazindikira momwe Satana amaukira mochenjera! Ngati wina aliyense amvetsera manong'onong'o a satana, ndiye Satana amapitiriza kumuvutitsa. Kunyalanyaza ndi kusapereka chidwi ku manong'onong'o ake ndi machiritso ake. Komanso, munthu ayenera kupempha chitetezo cha Allah عَزَّوَجَلَّ nthawi zonse ku zoyipa za Satana. Zakhala zowonekeratu kuti munthu ayenera kukhala wophunzira wa mtsogoleri aliyense wangwiro wa uzimu chifukwa chidwi cha mtsogoleri wa uzimu chimatetezanso ku manong'onong'o a satana.

*Hay 'Attar ko salb-e-Iman ka dharka*

*Bacha is ka Iman bacha Ghaus-e-A'zam*



www.dawateislami.net

*Kumasulira: 'Attar akuwopa kutaya chikhulupiriro chake. O Ghaus-e-A'zam! Chonde tetezani chikhulupiriro chake.* *(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 296)*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب        صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Manong'onong'o a satana okhudza tsogolo (chikonzero)

Satana amapitirizanso kuyambitsa manong'onong'o mu ntima okhudza tsogolo. Mwachitsanzo, amati, "Ndife wokakamizidwa kuchita chilichonse chomwe tinakonzedweratu kuti tichite. Tilibe mphanvu polimbana ndi tsogolo. Tikuchita ndendende zomwe zinalembedwa m'tsogolo lathu. Ndiye, n'chifukwa chiyani kuli chilango cha m'manda ndi Gehena ndi zina zambiri?"

Ndithudi, ichinso ndi chinyengo cha Satana. Musayesenso kuganizira za izi, apo ayi Satana adzakusocheretsani. Muthamangitseni powerenga ﴿اَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْم﴾.

## Zomwe wina adzachite zinalembedwa kale m'chikonzero

Abale okondedwa achisilamu! Kumbukirani! Allah عَزَّوَجَلَّ anadziwa kale ndipo nthawi zonse amadziwa zomwe aliyense adzachite ndipo Allah عَزَّوَجَلَّ analemba tsogolo lawo motero. Ntchito ya Mulungu yodziwa ndi kulemba simamukakamiza

aliyense kuchita chilichonse. Yesetsani kunvetsetsa ndi chitsanzo chosavuta ichi. Masiku ano, tsiku lotha ntchito limasindikizidwa monga lamulo pa zitini kapena makatoni a chakudya ndi mapaketi a machiritso ndi zina zambiri. Ngakhale mwana amatha kunvetsetsa kuti opanga amatchula tsiku lotha ntchito chifukwa amadziwa kuchokera mu kuzindikira kuti chinthu chinachake chidzawonongeka mpaka tsiku linalake. Choncho, amatchula tsiku lotha ntchito. Ndithudi, opanga chinthu kutchula tsiku lotha ntchito sikukakamiza chinthucho kuwonongeka. Ngakhale anakapanga kutchula tsiku lake lokutha ntchito, chinthucho chikanatha kuwonongeka pambuyo pa tsiku lotchulidwalo.

## Fatwa yofunika yokhudza tsogolo (chikonzero)

Zanenedwa pa tsamba 583 mpaka 585 la buku la masamba 692 la Kufriyah Kalimat kay baaray mayn Suwal Jawab [ Mafunso ndi Mayankho okhudza Mawu Onyoza] losindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah, nthambi yosindikiza ya Dawat-e-Islami: Ndi Fatwa yotengedwa pa tsamba 284 ndi 285 a buku la 29 la Fatawa Razawiyyah ndipo aperekedwa pano monga funso ndi yankho lake.

Funso: Zayd akunena kuti chilichonse chinachitika ndipo chidzachitika ndi lamulo la Allah عَزَّوَجَلَّ. N'chifukwa chani kapolo akutsutsidwa ndipo n'chifukwa chani amakhala woyenera kulandira chilango? Kodi walakwa chani kuti akhale woyenera chilango? Zomwe Allah عَزَّوَجَلَّ analemba m'chikonzero ndizomwe zimachitika. Izi zikutsimikiziridwa ndi Quran

Yopatulika kuti ngakhale kachinthu kakang'ono sikangathe kuyenda popanda lamulo la Mulungu. Kodi kapolo walakwa chiyani mwadala kuti akhale wokhala m'Gehena kapena wosakhulupirira kapena wolakwa? Ngati adakonzedweratu kuti achite zabwino, adzachita zabwino. Ndipo ngati adakonzedweratu kuti achite zoyipa, adzachita zoyipa. Mulimonse momwe zinthu ziliri, amakakamizika kuchita zomwe zinalembedwa m'tsogolo lake. N'chifukwa chiyani ndiye amatchedwa wochita zoyipa? Ngati zoyipa monga kuba, chigololo ndi kupha ndi zina zambiri. zalembedwa m'tsogolo lake, ndithudi adzazichita. Ngati zabwino zalembedwa m'tsogolo lake, adzazichitanso.

Yankho: Zayd ndi wopotoka komanso wosochera. Ngati wina wamumenya ndi nsapato, n'chifukwa chani amakwiya? Izinso zinalembedwa m'tsogolo lake. Ngati wina amubera ndalama, n'chifukwa chani amakwiya? Izinso zinalembedwa m'tsogolo lake. Kuganiza kuti tiyenera kuchita zomwe zalembedwa m'tsogolo lathu ndi chinyengo cha satana (ndipo si zoona). Kwenikweni, Allah عَزَّوَجَلَّ ankadziwa kale zomwe tidzachite ndipo Iye عَزَّوَجَلَّ analemba motero.

Katswiri wodziwika komanso wotsogola wa Shari'ah ndi Tareeqah, 'Allamah Maulana Mufti Muhammad Amjad 'Ali A'zami رحمۃاللہعلیہ anafotokoza pa tsamba 24 la buku loyamba la buku la Bahar-e-Shari'at losindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah: Kuchita choyipa ndikuchigwirizanitsa ndi chikhonzero ndikunena kuti ndi zotsatira za chifuniro cha Mulungu ndi chinthu choyipaa kwambiri. Ngati wina wachita

chabwino, amalamulidwa kuti achitenge ngati chisomo cha Allah عَزَّوَجَلَّ ndipo ngati wachita choyipa, ayenera kuchitenga ngati cholakwa cha Nafs yake [umunthu wake wamkati].

## Machiritso abwino a manong'onong'o a satana okhudza tsogolo

Nachi chidule cha Vesi yotengedwa pa tsamba 86 ndi 87 la buku la masamba 344 la Minhaj-ul-'Aabideen lolembedwa ndi Sayyiduna Imam Muhammad Ghazali رَحْمَةُاللّٰهِعَلَيْه losindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah, nthambi yosindikiza ya Dawat-e-Islami: Nthawi zina, Satana amasocheretsa anthu poyambitsa manong'onong'o monga: 'Kaya munthu ali ndi mwayi kapena tsoka zinasankhidwa tsiku loyamba. Amene anali ndi tsoka tsiku limenero adzakhalabe ndi tsoka ndipo amene anali ndi mwayi tsiku limenero adzakhalabe ndi mwayi. Ntchito zanu zabwino ndi zoyipa sizingasinthe chikonzero cha tsogolo.'

Ngati Allah عَزَّوَجَلَّ ateteza kapolo ku manong'onong'o a satana ndipo kapoloyo apereka yankho ili kwa Satana wotembereredwa: 'Ndine kapolo wa Allah عَزَّوَجَلَّ ndipo kapolo ayenera kutsatira lamulo loperekedwa ndi Mlengi Wake. Popeza Allah عَزَّوَجَلَّ ndiye Mbuye wa zolengedwa zonse, Iye عَزَّوَجَلَّ amapereka lamulo lomwe Iye عَزَّوَجَلَّ amafuna ndipo amachita zimene Iye عَزَّوَجَلَّ akufuna. Komanso, ntchito zopembedza ndi kumvera sizowopsa mwanjira iliyonse. Ngati ndili wamwayi mu mukudziwa kwa Mulungu, ngakhale pamenepo ndikufunika



www.dawateislami.net

mphoto yochuluka. Ndipo Allah عَزَّوَجَلَّ aletse, ngati dzina langa lalembedwa pakati pa opanda mwayi mu mukudziwa kwa Mulungu, ndidzakhalabe ndikuchita ntchito zabwino kuti ndisadzachite manyazi ozunzidwa chifukwa chosowa ntchito zabwino. Ndipo kupita ku Gehena ndi kumvera ndibwino kuposa kupita ku Gehena ndi kusamvera.

Zowona zake, zonsezi ndi zongokayikira chabe chifukwa lonjezo ndi Mawu a Allah عَزَّوَجَلَّ ndi owona ntima. Allah عَزَّوَجَلَّ wapanga malonjezo angapo opatsa mphoto yochuluka pa kumvera ndi ntchito zopembedza (zabwino). Choncho, aliyense amene adzadziwonetse yekha m'bwalo la Mulungu ndi chikhulupiriro ndi kumvera sadzalowa Gehena. M'malo mwake, adzapatsidwa malo okhala ku Jannat-ul-Firdaus mwa chisomo cha Allah عَزَّوَجَلَّ kudzera mu ntchito zabwino, اِنْ شَآءَاللّٰه عَزَّوَجَلَّ. Kwenikweni, adzalowa Kumwamba chifukwa cha lonjezo la Mulungu. Posonyeza lonjezo lomweli lowona ntima, Allah عَزَّوَجَلَّ watchula mawu a anthu amwayi mu Vesi 74 ya Surah Az-Zumar, gawo 24 la Quran Yopatulika:

وَ قَالُوا الۡحَمۡدُ لِلّٰهِ الَّذِیۡ صَدَقَنَا وَعۡدَهٗ

*Ndipo iwo adzanena, 'Matamando onse ali kwa Allah Amene wakwaniritsa lonjezo Lake kwa ife.'*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 24, Surah Az-Zumar, Vesi 74)*

*Allah ki rahmat say to Jannat hi milay gi*

*Ay kash! Mahallay mayn jagah un kay mili ho*

*Kumasulira: Tidzalowa Kumwamba mwa chifundo cha Allah عَزَّوَجَلَّ. Ngati tingapeze malo okhala pafupi ndi Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم.*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Manong'onong'o a satana okhudza chikhulupiriro

Abale achisilamu okondedwa! Nthawi zina, Satana amayambitsa manong'onong'o amene munthu sangakwanitse kuwafotokoza ndi mawu. Monga momwe Masahaba odalitsika رضی اللہ عنہم nthawi zonse ankakhala otanganidwa kumvera Allah عَزَّوَجَلَّ ndi Mtumiki Wake صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم Satana ankawavutitsa kwambiri kudzera m'manong'onong'o.

Zafotokozedwa m'buku la Hadees la Sahih Muslim kuti ena mwa Masahaba odalitsika رضی اللہ عنہم anabwera pa maso pa Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndipo ananena modzichepetsa, 'Tili ndi maganizo otere (manong'onong'o a satana) m'mitima mwathu omwe tikumawawona kuti ndi oyipa kwambiri kuwafotokoza.' Mtumiki Wolemekezeka ndi Wodziwika صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Kodi mukumazinva zimenezi?' Iwo ananena modzichepetsa, 'Inde.' Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Ichi ndi chikhulupiriro chodziwika.'

*(Sahih Muslim, tsamba. 80, Hadees 132)*

## Manong'onong'o owopsa a satana

Munthu wina anabwera pa maso pa Mtumiki Wamkulu ndi Wolemekezeka Kwambiri صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndipo anati modzichepetsa, 'Ndiri ndi maganizo otere muntima mwanga omwe ndinakakonda kuwotchedwa kuti ndikhale phulusa m'malo mowafotokoza.' Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Tikuthokoza Allah عَزَّوَجَلَّ Amene anawapanga maganizowa kukhala manong'onong'o a satana.' *(As-Sunnah li Abi 'Aasim, tsamba. 157, Hadees 670)*

Wofotokoza wodziwika, woganiza mozama wa Ummah, Mufti Ahmad Yar Khan رحمۃ اللہ علیہ ananena kuti Allah عَزَّوَجَلَّ wawafotokoza maganizowa kukhala manong'onong'o a satana ndipo palibe chilango chake. Iye عَزَّوَجَلَّ ndi Wachisomo ndipo amadziwa kufowoka kwa kapolo.' *(Mirat-ul-Manajih, buku. 1, tsamba. 86)*

## Palibe chilango pa manong'onong'o a satana

Sayyiduna Abu Hurayrah رضی اللہ عنہ anafotokoza kuti Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Ndithudi Allah عَزَّوَجَلَّ wawakhululukira maganizo (manong'onong'o oyambitsidwa ndi Satana) m'mitima mwa Ummah wanga chifukwa cha ine; pokhapokha atachita zinthu molingana ndi manong'onong'owo ndikulankhula za iwo.' *(Sahih Bukhari, buku. 2, tsamba. 153, Hadees 2528)*

Pothirira ndemanga pa Hadees yomwe ili m'mwambayi, wofotokoza wodziwika, woganiza mozama wa Ummah, Mufti Ahmad Yar Khan رحمۃ اللہ علیہ anati, 'Palibe chilango pa maganizo

oyipa. Zimenezi makamaka mu Ummah uwu. Ma Ummah am'mbuyomu ankayimbidwa mlandu ngakhale pa iwo (chifukwa chokhala ndi manong'onong'o a satana mosalekeza muntima kapena kuganizira za iwo mwadala.

Kumbukirani kuti pali kusiyana pakati pa lingaliro loyipa ndi cholinga choyipa chokhazikika. Munthu amayankha mlandu pa cholinga choyipa chokhazikika. Ngakhale cholinga chokhazikika cha kusakhulupirira ndi 'kusakhulupirira'.

*(Mirat-ul-Manajih, buku. 1, tsamba. 81)*

## Kuthekera kwa chilango pa manong'onong'o a satana

Wofufuza wovomerezeka mogwirizana wa sayansi ya Chisilamu, katswiri wophunzira za Chisilamu wotsogola wa Hadees, 'Allamah 'Abdul Haq Muhaddis Dihlvi رحمۃ اللہ علیہ anena kuti: Lingaliro loyipa lomwe limabwera muntima mwadzidzidzi limatchedwa ﴿هَاجِس﴾ [Hajis]. Limakhalapo muntima kwa kanthawi kochepa ndipo limatha. Ma Ummah am'mbuyomu anakhululukidwa pa lingaliro limeneli ndipo ifenso timakhululukidwa. Komabe, ife tokha ndi amene timakhululukidwa pa lingaliro lomwe limakhalabe muntima; iwo sanakhululukidwe pa zimenezi. Ngati palinso chisangalalo ndi chimwemwe limodzi ndi lingaliro muntima, ndiye limeneli limatchedwa ﴿هَمّ﴾ [Hamma]. Palibenso chilango ngakhale pa ilo. Ngati pali chitsimikizo chokhazikika choyichita ntchito

molingana ndi lingaliro loyipa lomwe lakhalapo muntima, ndiye pali chilango chake.

*(Ashi'a-tul-Lam'aat, buku. 1, tsamba. 85)*

## Chikhulupiriro sichiwonongedwa ndi manong'onong'o a satana

Zilibe kanthu kuti ndi manong'onong'o angati komanso owopsa a satana omwe munthu amakumana nawo, chikhulupiriro chake sichiwonongedwa nawo. Kukhala ndi nkhawa muntima chifukwa chokumana ndi manong'onong'o a satana okhudza chikhulupiriro kumasonyeza kuti ntima uli wokhazikika ndi chikhulupiriro. Mu Vesi 106 ya Surah An-Nahl, Allah عَزَّوَجَلَّ wanena mu gawo 14:

وَ قَلْبُهٗ مُطْمَىٕنٌّۢ بِالْاِیْمَانِ

*Ndipo ntima wake uli wokhazikika m'chikhulupiriro.*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 14, An-Nahl, Vesi 106)*

## Kuwona manong'onong'o a satana ngati oyipa ndi chikhulupiriro chenicheni

Abale achisilamu okondedwa! Kukumana ndi manong'onong'o a satana okhudza chikhulupiriro ndi chizindikiro cha ungwiro wa chikhulupiriro. Akuba ndi achifwamba amabwera komwe

kuli chuma chochuluka. Choncho, chikhulupiriro cha munthu chikakhala cholimba, m'pamenenso Satana amamuvutitsa kwambiri. Ngati Msilamu ali ndi nkhawa ndi kudandawula pokumana ndi manong'onong'o a satana ndipo akupempha chitetezo cha Allah عَزَّوَجَلَّ kuchokera kwa Satana wotembereredwa, ichi ndi chizindikiro cha chikhulupiriro cholimba.

Katswiri wophunzira za Chisilamu wodziwika pa nkhani za chipembedzo, woganiza kwambiri wa Ummah, Mufti Ahmad Yar Khan رحمۃ اللہ علیہ anati, 'Kuwatenga manong'onong'o a satana ngati oyipa ndi chikhulupiriro chenicheni.' *(Mirat-ul-Manajih, buku. 1, tsamba. 82)*

*Istiqamat di-jiye Islam per*

*Ki-jiye rahmat ay Nana-e-Husayn*

*Dil say dunya ki hawas sab door ho*

*Ki-jiye rahmat ay Nana-e-Husayn*

*Naz'a, qabr-o-hashr, meezan her jagah*

*Ki-jiye rahmat ay Nana-e-Husayn*

Kumasulira: O Agogo aamuna (صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم) a Sayyiduna Imam Husayn رضی اللہ عنہ! Ndichitireni chifundo pondidalitsa ndi kukhazikika m'chikhulupiriro ndi kuchotsa dyera la dziko



www.dawateislami.net

lapansi mu ntima mwanga. Komanso ndichitireni chifundo m'manda, pa Tsiku la Kuwuka kwa Akufa, pa Tsikelo ndi malo ena aliwonse.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب      صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Manong'onong'o a satana pa nthawi ya kulambira

Monga momwe Satana amayambitsira manong'onong'o okhudza chikhulupiriro, amayambitsanso manong'onong'o pa nthawi ya ntchito zolambira. Iye sali yekha pa nkhaniyi; m'malo mwake, pali gulu lokonzedwa bwino limodzi ndi iye.

Othirira ndemanga wodziwika, woganiza bwino wa Ummah, Mufti Ahmad Yar Khan رحمۃ اللّٰہِ علیہ anena kuti, 'Pali magulu osiyanasiyana a ana a Satana okhala ndi mayina ndi ntchito zosiyanasiyana. Gulu lomwe limayambitsa manong'onong'o pa nthawi ya Wudu limatchedwa ﴿وَلْهَان﴾ [Walhaan] ndipo gulu lomwe limayambitsa manong'onong'o pa nthawi ya Salah limatchedwa ﴿خِنْزَب﴾ [Khinzab]. Mwanjira yofanana, magulu ankhondo a satana amakhala M'mizikiti, m'misika ndi m'mabala a Mowa.'

*(Mirat-ul-Manajih, buku. 1, tsamba. 85)*

## Mayina a Asatana 9 ndi ntchito zawo

Zanenedwa pa tsamba 40 ndi 41 la buku la masamba 1548



www.dawateislami.net

lotchedwa Faizan-e-Sunnat [Madalitso a Sunnah] losindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah, nthambi yosindikiza ya Dawat-e-Islami: Mtsogoleri wa okhulupirira, Sayyiduna 'Umar Farooq-e-Azam رضی اللہ عنہ ananena kuti Satana ali ndi ana 9: (1) ﴿زَلِيْتُوْن﴾ [Zalitoon] (2) ﴿وَثِيْن﴾ [Waseen] (3) ﴿لَقُوْس﴾ [Laqoos] (4) ﴿اَعْوَان﴾ [Awaan] (5) ﴿هَفَّاف﴾ [Haffaaf] (6) ﴿مُرَّة﴾ [Murrah] (7) ﴿مُسَوِّط﴾ [Musawwit] (8) ﴿دَاسِم﴾ [Daasim] (9) ﴿وَلْهَان﴾ [Walhaan].

1. Zalitoon amayikidwa m'misika komwe amayika mbendera yake.
2. Waseen amayikidwa kuti apangitse anthu kuvutika ndi mavuto osayembekezereka.
3. Laqoos amayikidwa kwa anthu opembedza moto.
4. A'waan amayikidwa kwa olamulira.
5. Haffaaf amayikidwa kwa omwa mowa.
6. Murrah amayikidwa kwa anthu oyimba nyimbo ndi kuyimba zida zoyimbira.
7. Musawwit amayikidwa kuti azifalitsa mphekesera. Amapangitsa anthu kukhulupirira ndi kufalitsa mphekesera, kuwapangitsa kuti asadziwe chowonadi.
8. Daasim amayikidwa m'nyumba. Ngati munthu

sanawerenge ﴿بِسْمِ اللّٰهِ﴾ polowa m'nyumba yake, kapena sanapereke Salam akamalowa, ndiye Satana uyu amayambitsa mikangano m'banja, ngakhale kuyambitsa chisudzulo kapena Khula' (nkazi kupempha kuti banja lithe) kapena kumenyana.

9. Walhaan amayikidwa kuti ayambitse manong'onong'o a satana muntima mwa munthu pa nthawi ya Wudu. *(Al-Munabbihat, tsamba. 93)*

*Nafs-o-shaytan ho gaye ghalib*

*In kay chungal say Tu chhura Ya Rab*

*Kumasulira: O Ambuye! Nafs ndi Satana andilamulira ine. Chonde ndimasuleni ku ukapolo wawo.*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Manong'onong'o a satana M'mizikiti

Kampeni ya satana ya manong'onong'o ndi yamphanvu kwambiri M'mizikiti. Amapangitsa Asilamu ambiri kuchita nawo zokambirana zapadziko lapansi M'mizikiti. Amapangitsanso ena a iwo kukangana wina ndi nzake ndipo amapangitsa anthu achikulire kukwiya, kuwapangitsa kupanga phokoso M'mizikiti. مَعَاذَ اللّٰه عَزَّوَجَلَّ amapangitsa ena a iwo kuchita machimo monga kuyang'ana kosaloledwa, makhalidwe oyipa, miseche, kufalitsa nkhani yabodza komanso zina zambiri. Ngati

walephera kuwapangitsa ena a iwo kuchita machimo, Satana amawapangitsa kukhala awulesi m'ntchito zabwino. Aliyense ayenera kuti anakumana nazo. Mwachitsanzo, pa nthawi ya Dars ndi ulaliki zoperekedwa M'mizikiti, anthu ena amakhala M'mizikiti komano amakhala patali kwinaku akuyang'ana uku ndi uku mosasamala ndi kudzimana madalitso a Dars kapena ulaliki. Amene amakhala onyalanyaza pa kumukumbukira Mulungu komanso amakhala awulesi popita ku magawo ophunzirira za maphunziro a Chisilamu ndi zina zambiri ngakhale ali M'mizikiti ayenera kuwerenga mosamala Hadees yotsatirayi yomwe yatchulidwa mu Fatawa Razawiyyah:

Sayyiduna Abu Hurayrah رضی اللّٰہ عنہ anafotokoza kuti Mtumiki Wokondedwa ndi Wodalitsika صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Pamene aliyense wa inu ali mu nzikiti, Satana amabwera kwa iye ndikumusisita thupi lake, monga momwe mumasisitira kavalo wanu kuti akhale wonvera. Ngati munthuyo apitiriza kukhala (ngati sakukana manong'onong'o a satana nthawi yomweyo), ndiye Satana amamumanga ndi chingwe.'

Sayyiduna Abu Hurayrah رضی اللّٰہ عنہ ananena kuti, 'Zowona za Hadees iyi zingatsimikizidwe poyang'ana nkhalidwe la anthu. Mudzawona kuti amene wamangidwa [ndi Satana] akuwerama ndipo sakuchita Zikr za Mulungu. Ndipo amene wapatsidwa chingwe [ndi Satana] watsegula pakamwa pake ndipo sakuchita Zikr za Allah عَزَّوَجَلَّ *(Musnad Imam Ahmad, Hadees 8378; Fatawa Razawiyyah – yotchulidwa, buku. 1, masamba 771-772)*

*Ganday ganday wasawis aatay hayn*

*Mayray dil say inhayn nikaal Aqa*

*Kumasulira: Satana amayambitsa manong'onong'o onyansa. O Bwana wanga) صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم!! Achotseni mu ntima mwanga.*

*(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 209)*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب     صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Manong'onong'o a satana pa nthawi ya Ghusl

Satana amayambitsanso kukayikira pa nthawi ya Ghusl. Mwachitsanzo, nthawi zina munthu wosamba amaganiza kuti nsana wake mwina sunasambitsidwe. Mwina tsitsi la pamutu silinasambitsidwe bwino; gawo lina la thupi lidalibe louma ndi zina zambiri. Kwenikweni, izi si zolondola. Ngati munthu wasambitsa gawo la thupi bwinobwino kulipukuta bwino, palibe chifukwa chokhala ndi kukayikira kulikonse.

## Choyambitsa manong'onong'o a satana pa nthawi ya Ghusl

Kumbukirani! Kukodza m'malo osambira m'bafa kumayambitsa manong'onong'o a satana. Choncho, munthu ayenera kupewa. Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, ‘Munthu asakodze konse m'bafa chifukwa adzasamba kapena kuchita

Wudu m'menemo. Izi zili choncho chifukwa manong'onong'o a satana amayambitsidwa ndi izi.'

*(Sunan Abi Dawood, buku. 1, tsamba. 44, Hadees 27)*

## Kufotokozera kwa Hadees yomwe yatchulidwa pamwambapa

Zanenedwa pa tsamba 201 ndi 202 la buku la masamba 308 la Islami Behno ki Namaz [Salah ya Alongo Achisilamu] losindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah, nthambi yosindikiza ya Dawat-e-Islami: Pofotokoza Hadees yomwe yatchulidwa, wofotokoza wodziwika, woganiza kwambiri wa Ummah, Mufti Ahmad Yar Khan رحمۃ اللہ علیہ ananena kuti, 'Palibe vuto kukodza m'malo osambira ngati ali ndi pansi pa simenti kapena nsangalabwi pokhala ndi malo otsetsereka bwino ndi ngalande. Komabe, ndibwinobe kupewa. Koma ngati alibe pansi potere ndi ngalande, ndiye kukodza malo otere ndi zoyipa kwambiri chifukwa pansi padzakhala podetsedwa, ndipo thupi lidzathiridwa madzi odetsedwa pa nthawi yosamba kapena Wudu.

Hadees iyi imatanthawuza za nkhani yachiwiri, chifukwa kuletsa kumatsindikizidwa kwambiri. Zapezeka kuti kukodza m'malo oletsedwa kumayambitsa manong'onong'o a satana kapena kukayikira za nkodzo kuwaza pa thupi.' *(Mirat-ul-Manajih, buku. 1, tsamba. 266)*

## Fanizo lonena za vuto loyambitsidwa ndi manong'onong'o a satana

Potchula machiritso othandiza a manong'onong'o a satana, mbuye wanga A'la Hadrat, mtsogoleri wa Ahl-e-Sunnah, Maulana Shah Imam Ahmad Raza Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena pa tsamba 1043 mu gawo 'B' la buku loyamba la Fatawa Razawiyyah kuti: Kusapereka chidwi ku manong'onong'o a satana, kusachita zinthu molingana nawo ndikutsutsana nawo [ndi machiritso ake]. Nthawi zambiri, munthu akamapereka chidwi kwambiri ku manong'onong'o a satana, m'pamenenso amakumana ndi manong'onong'o ochuluka. Komano, ngati munthu akutsutsana ndi manong'onong'o a satana mwadala, amazimiririka nkati mwa nthawi yochepa kwambiri, mwa lamulo la Allah عَزَّوَجَلَّ. Sayyiduna Amr Bin Murrah رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ anati, 'Ngati Satana wawona kuti manong'onong'o ake akukhudza wina aliyense; amamuvutitsa munthu wotere kwambiri.'

*(Musannaf Ibn Abi Shaybah, buku. 1, tsamba. 224)*

Imam Ibn Hajar Makki رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena mu' 'Fatawa' yake: Anthu ena odalirika anandiwuza kuti anthu awiri omwe nthawi zambiri ankaganizira za manong'onong'o a satana ankafuna kusamba. Anapita ku mtsinje wa Nile m'mawa kwambiri. Mmodzi wa iwo anati kwa mnzake. Pita iwe ukalowe m'madzi; ine ndikhala ndikukuwona komanso kukuwuza ngati thupi lako lonse lasambitsidwa kapena ayi. Anapita ndikuyamba kulowa m'madzi. Munthu winayo woyima kunja kwa madzi anati,



www.dawateislami.net

'Kachigawo kakang'ono ka mutu wako kadakali kowuma; kachigawo kena ka thupi n'kowuma.' Munthu wosambayo anapitiriza kusamba kuyambira m'mawa mpaka masana. Pamapeto pake, anabwerera, atatopa ndipo akukayikira ngati Ghusl yake ndi yovomerezeka kapena ayi. Kenako anati kwa munthu winayo, 'Tsopano pita iwe ndipo ine ndikhala ndikukuwona komanso kukuwuza.' Munthu winayo nayenso analowa m'madzi ndipo munthu woyimayo anati, 'Mutu wako sunasambitsidwebe.'

Izi zinapitirira mpaka madzulo unafika. Pamapeto pake, munthu winayo nayenso anabwerera ndi kukayikira muntima mwake za Ghusl. Onse awiri anaphonya Salah za tsiku lonse ndipo anakhalabe okayika za Ghusl. ﴿وَالْعِيَاذُ بِاللّٰهِ تَعَالٰى﴾ (tikupempha chitetezo cha Allah عَزَّوَجَلَّ) Ichi ndi chotsatitira chopereka chidwi ku manong'onong'o a satana.

*(Hadeeqah Nadiyyah Sharh Tareeqah Muhammadiyyah, buku. 2, tsamba. 691)*

*Mujhay waswason say bacha Ya Ilahi*

*Pa-ay Ghaus-o-Ahmad Raza Ya Ilahi*

*Kumasulira: O Wamphanvu zonse! Nditetezeni ku manong'onong'o a satana chifukwa cha Ghaus ndi Raza* رحمهما الله.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد



www.dawateislami.net

## Manong'onong'o a satana pa nthawi ya Wudu

Satana wotchedwa 'Walhaan' amayambitsa manong'onong'o osiyanasiyana okhudza Wudu. Mwachitsanzo, amayambitsa manong'onong'o otere muntima mwa munthu wochita Wudu monga: 'Gawo lina la thupi lasiyidwa losasambitsidwa; gawo lina la thupi lasambitsidwa kawiri m'malo mwa katatu.' Chimodzimodzinso, ngati Wudu wa munthu udakali ovomerezeka, Satana uyu amayambitsa manong'onong'o otere monga: 'Wudu wako waduka; nthawi yochuluka yadutsa kuchokera pamene unachita Wudu, choncho, Wudu wako mwina waduka' ndi zina zambiri. Muzochitika zotere, munthu sayenera kupereka chidwi ku manong'onong'o a satana konse.

Ponena za Satana amene amayambitsa manong'onong'o pa nthawi ya Wudu, Mtumiki Wokondedwa ndi Wodalitsika صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Pali Satana wotchedwa 'Walhaan' amene amayambitsa manong'onong'o pa nthawi ya Wudu. Motero, mumakhala otetezeka ku manong'onong'o a satana okhudza madzi.'

*(Sunan Ibn Majah, buku. 1, tsamba. 252, Hadees 421)*

## Kuwaza madzi pa gawo la thalawuza

Pambuyo pa Wudu, ngati wina akukayikira kuti dontho lililonse la nkodzo lituluka, munthu akhoza kudziteteza ku manong'onong'o a satana powaza madzi pa gawo la thalawuza



www.dawateislami.net

pafupi ndi ziwalo zobisika. Sayyiduna Abu Hurayrah رضی اللہ عنہ anafotokoza kuti Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Mukamachita Wudu, muyenera kuwaza madzi.'

*(Sunan Ibn Majah, buku. 1, tsamba. 270, Hadees 463)*

Ngati akukumanabe ndi manong'onong'o a satana, ayenera kuganiza yekha kuti awa ndi madzi omwe anawaza. Komabe, ngati wina watulukadi madontho a nkodzo, imeneyi ndi nkhani ina.

## Zoyenera kuchita ngati wina akumana ndi manong'onong'o a satana pa nthawi ya Wudu?

Katswiri wophunzira za Chisilamu wodziwika komanso wotsogola wa Shari'ah ndi Tareeqah, 'Allamah Maulana Mufti Muhammad Amjad 'Ali A'zami رحمۃ اللہِ علیہ anafotokoza pa tsamba 310 la buku loyamba la masamba 1250 la Bahar-e-Shari'at losindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah, nthambi yosindikiza ya Dawat-e-Islami kuti: Ngati wina akukayikira ngati gawo lililonse la thupi lasambitsidwa kapena ayi pa nthawi ya Wudu, ayenera kulisambitsa, ngati ili nthawi yoyamba m'moyo wake. Ngati nthawi zambiri amakayikira, sayenera kupereka chidwi. Chimodzimodzinso, ngati wina akukayikira atachita Wudu ngati Wudu wake unakalipo kapena ayi, palibe chifukwa chochitira Wudu panthawiyi. Komabe, ndibwino kuchita Wudu pamene kukayikira sikunayambitsidwe ndi



www.dawateislami.net

manong'onong'o a satana. Ngati ndi manong'onong'o a satana, sayenera kuwatsatira konse. Ngati wina achita Wudu panthawiyi poganiza kuti akusamala, izi zilibe chochita ndi kusamala, koma ndi kunvera Satana wotembereredwa.

*Tu Wudu kay waswason say Ya Khuda mujh ko bacha*

*Sath zaahir kay mayra baatin bhi ho jaye safa*

*Kumasulira: O Wamphanvu zonse! Nditetezeni ku manong'onong'o a satana pa nthawi ya Wudu. Umunthu wanga wankati pamodzi ndi wanga wakunja nawonso uyeretsedwe!*

## Manong'onong'o a satana okhudza kuwonongeka kwa Wudu pa nthawi ya Salah

Nthawi zina, Satana amayambitsa manong'onong'o pa nthawi ya Salah monga Wudu wako wawonongeka; watulutsa dontho la nkodzo kapena watulutsa mpweya. M'nkhaniyi, pambuyo potchula Mahadees ena, mbuye wanga A'la Hadrat, wotsitsimutsa Sunnah, wochotsa Bid'ah, katswiri wa Shari'ah, Maulana Shah Imam Ahmad Raza Khan رحمۃ اللہ علیہ ananena kuti: Mathero ochokera ku Mahadees awa ndi akuti Satana nthawi zina amalavulira pa maliseche akutsogolo kuti anyenge munthu wopemphera Salah, kumupangitsa kukayikira kuti watulutsa dontho la nkodzo. Nthawi zina, Satana amawuzira pa maliseche akumbuyo kapena kukoka tsitsi, kupangitsa munthu wopemphera Salah kukayikira kuti watulutsa mpweya. Ngati



www.dawateislami.net

mukunva mitundu iyi ya manong'onong'o a satana, munthu akulamulidwa kuti asasiye Salah yake pokhapokha atawona kunyowa, kunva phokoso kapena fungo komanso pokhapokha atatsimikiza kuti Wudu wake waduka.

*(Fatawa Razawiyyah – yotchulidwa, buku. 1, tsamba. 774)*

## Nena kwa Satana 'ndiwe wabodza'

Abale achisilamu okondedwa! Wudu umakhalabe wovomerezeka pokhapokha wina atatsimikiza kuti akhoza kulumbira za kuwonongeka kwake. Ngati Satana akunena kuti: 'Wudu wako waduka kapena wawonongeka'. Munthu ayenera kumuyankha muntima mwake kuti: 'O woyipa iwe! Iwe ndiwe wabodza.' Munthu ayenera kupitiriza Salah yake.

Sayyiduna Abu Sa'eed Khudri رضی اللّٰہ عنہ anafotokoza kuti Mtumiki Wankulu ndi Wolemekezeka Kwambiri صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati: Satana akabwera kwa aliyense wa inu ndikunena kuti Wudu wako wawonongeka; munthu ayenera kumuyankha nthawi yomweyo muntima kuti, 'Ndiwe wabodza'; pokhapokha atanva phokoso kuchokera m'makutu ake kapena kununkhiza fungo ndi mphuno yake.

*(Al-Ihsaan bittarteeb Sahih Ibn Hibbaan, buku. 4, tsamba. 153, Hadees 2656)*

## Ine komanso ntchito yanga si ife angwiro

Bwana wanga A'la Hadrat, mtsogoleri wa Ahl-e-Sunnah,

Maulana Shah Imam Ahmad Raza Khan رحمۃ اللہ علیہ ananena kuti: Ngakhale pambuyo pake, ngati Satana wayambitsa manong'onong'o akuti simunachite ntchito mwangwiro chifukwa pali cholakwika ichi ndi ichi, munthu ayenera kuyankha Satana m'mawu awa: 'Usandiwonetsere chifundo konse. Palibe chifukwa chondilangiza. Ngati ntchito yanga si yangwiro, inenso sindine wangwiro. Ndayichita momwe ndingathere. Mbuye wanga (عَزَّوَجَلَّ) ndi Wachisomo ndipo amadziwa kufowoka kwanga. Pondichitira chifundo, Iye عَزَّوَجَلَّ adzalandira ntchito iyi. Ndani angachite ntchito molingana ndi ulemerero ndi ukulu wa Allah عَزَّوَجَلَّ!

Ngati manong'onong'o a satana sakutha ngakhale mutachita izi, munthu ayenera kunena kwa Satana kuti: 'Ngati ukunena kuti Wudu wanga ndi Salah yanga siziri zovomerezeka, ziribe kanthu. Ndakonzeka kupemphera Salah popanda Wudu kapena kupemphera ma Rak'aat atatu a Zuhr Salah; monga momwe waganizira. O Wotembereredwa! Sindidzakunvera.' Ngati wina ali wotsimikiza kukana manong'onong'o a satana mwanjira imeneyi, manong'onong'o a satana adzatha. Satana adzalephera ndikuchititsidwa manyazi ndi thandizo la Mulungu.

*(Chidule chochokera mu: Fatawa Razawiyyah – yotchulidwa, buku. 1, 786-787)*

Sayyiduna Imam Mujahid رحمۃ اللہ علیہ ananenso kuti, 'Ndingakonde kupemphera Salah popanda Wudu kusiyana ndi kunvera Satana.' (Sizitanthawuza kuti munthu akhoza kupemphera Salah popanda Wudu. Kwenikweni, izi cholinga

chake ndikuchotsa manong'onong'o a satana.) *(At-Tareeqa-tul-Muhammadiyyah ma' Sharh Al-Hadeeqah An-Nadiyyah, buku. 2, tsamba. 688)*

## Kanani manong'onong'o a satana

Sayyiduna Ibraheem Nakhee رحمۃ اللہ علیہ anali mphunzitsi wa ma mphunzitsi a Sayyiduna Imam-e-Azam رحمۃ اللہ علیہ. Sayyiduna Ibraheem Nakhee رحمۃ اللہ علیہ ananena kuti: Musatsatire manong'onong'o a satana. Ngati akusokonezani kwambiri, ndiye munene kwa iye: 'Ndidzapemphera Salah ngakhale popanda Wudu ndipo sindidzakunverani.' Mwanjira imeneyi, Satana wotembereredwa amasiya kukuvutitsani. Mukamunvera, adzakusokonezani kwambiri.

*Mayn Tayri ita'at karun Ya Ilahi*
*Na shaytan ki hergiz sunu Ya Ilahi*

*Nthawi zonse ndizikunverani, O Wamphanvu zonse!*
*Sindidzanvera Satana, O Wamphanvu zonse!*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Manong'onong'o a satana pa nthawi ya Salah

Satana amapitirizanso kuyambitsa manong'onong'o kwa munthu wopemphera Salah, kumusokoneza maganizo pa Salah.



www.dawateislami.net

Zanenedwa m'buku la Sahih Muslim kuti Sayyiduna 'Usman Bin Abil 'Aas رضی اللّٰہ عنہ anati, 'Ndinanena modzichepetsa, "Ya Rasoolallah صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم! Ndimakapemphera Salah komanso kuwerenga, Satana amandisokoneza, kundipangitsa kukayikira za Salah.' Mtumiki Wokondedwa ndi Wodalitsika صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati, 'Satana uyu amatchedwa 'Khinzab'. Nthawi iliyonse wazindikira za izi, pempha chitetezo cha Allah عَزَّوَجَلَّ ndipo chita ngati ukulavulira kumbali yakumanzere katatu.' [Sayyiduna 'Usman Bin Abil 'Aas رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُ anati, 'Ndinachita monga ndinalangizidwira, choncho Allah عَزَّوَجَلَّ anandithandiza kuti ndimuchotse. *(Sahih Muslim, pp. 1209, Hadees 2203)*

## Njira yopewera manong'onong'o a satana pa nthawi ya Salah

Pothirira ndemanga pa Hadees yomwe ili pamwambayi, wofotokoza wodziwika, woganiza kwambiri wa Ummah, Mufti Ahmad Yar Khan رحمۃ اللّٰہ علیہ ananena kuti: Musananene Takbeer Tahrimah Salah ikamayamba, muyenera kuchita ngati mukulavulira kumbali yakumanzere katatu, kenako nenani ﴿لَا حَوۡلَ وَلَا قُوَّۃَ اِلَّا بِاللّٰہِ الۡعَلِیِّ الۡعَظِیۡمِ﴾, ndipo yang'anani malo ena ake pa nthawi ya zichitochito zina za Salah monga pamalo pa Sajdah pa nthawi ya Qiyam, pa mapazi [ pamwamba pa phazi pakati pa misomali ndi zala] pa nthawi ya Ruku', pa fupa la mphuno pa nthawi ya Sajdah, pa ntchafu pa nthawi ya Jalsah ( kukhala pakati pa ma Sujood awiri) ndi pa nthawi ya Qa'dah (Tashahhud



www.dawateislami.net

ndi zina zambiri), pochita zimenezi mudzatha kusunga kudzichepetsa kwa ntima, ntendere ndi kukhazikika pa nthawi ya Salah إِنْ شَآءَاللّٰه عَزَّوَجَلَّ. *(Mirat-ul-Manajih, buku. 1, tsamba. 89)*

## Malovu amagwera n'kamwa mwa Satana

Abale achisilamu okondedwa! Pali Hadees ina yomwe ili m'buku la 'Mishkat' m'mutu wa 'Bab-ul-Waswasah', mukunena kwina, mutu wa manong'onong'o a satana. Machiritso a manong'onong'o a satana ofotokozedwa mu Hadees yodalitsikayi ndi akuti munthu ayenera kuchita ngati akulavulira katatu kumbali yakumanzere.

Pofotokoza Hadees yodalitsikayi, wothirira ndemanga wodziwika, woganiza kwambiri wa Ummah, Mufti Ahmad Yar Khan رحمۃ اللّٰہِ علیه anati: Malovu awa adzagwera pankhope ya Satana, kumuchititsa manyazi ndikumuthamangitsa. Satana nthawi zambiri amabwera kuchokera kumbali yakumanzere. Izi zikusonyeza kuti nthawi zina Satana amathamangitsidwanso ndi malovu.

*(Mirat-ul-Manajih, buku. 1, tsamba. 88)*

اَلۡحَمۡدُلِلّٰه عَزَّوَجَلَّ ! Sag-e-Madinah عُفِیَ عَنۡهُ [wolemba] amakumana nazo nthawi zambiri kuti Satana amathawa mwamanyazi pamene ndimachita ngati ndikulavulira kumapewa anga akumanzere katatu ngati ndikunva manong'onong'o a satana m'chimbudzi. (Ndizoletsedwa kunena ﴿لَاحَوْل﴾ ndi mawu ena m'chimbudzi.)

*Na waswasay aayain na mujhay ganday khayalat*

*Ker zihn ka Allah 'ata Qufl-e-Madinah*

*Kumasulira: Nditha osakhala ndi manong'onong'o a satana kapena maganizo onyansa! O Allah عَزَّوَجَلَّ! Ndithandizeni kugwiritsa ntchito Qufl-e-Madinah ku maganizo anga!*

صَلُّوْاعَلَى الْحَبِيْب　　　　صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Manong'onong'o a satana okhudza chiwerengero cha ma Rak'aat mu Salah

Chifukwa cha manong'onong'o a satana pa nthawi ya Salah, munthu wopemphera Salah amakhala wokayikira za chiwerengero cha ma Rak'aat omwe wapemphera. Zafotokozedwa mu Hadees yodalitsika, 'Munthu wina anabwera pa maso pa Mtumiki Wokondedwa ndi Wodalitsika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndipo ananena modzichepetsa kuti amakumana ndi manong'onong'o a satana pa nthawi ya Salah ndipo amayiwala ngati wapemphera ma Rak'aat awiri kapena atatu.' Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Mukakumana ndi zoterezi, kwezani chala chanu cha dzanja lanu lamanja ndikuchimenya pa ntchafu yanu yakumanzere ndikunena ﴿بِسْمِ اللّٰهِ﴾. Izi zidzakhala ngati mpeni kwa Satana.' *(Al-Mu'jam-ul-Kabeer lit-Tabarani, buku. 1, tsamba. 192, Hadees 512)*

Choncho, amene amakumana ndi manong'onong'o a satana pa nthawi ya Salah nthawi zonse, ayenera kuchita izi asanayambe Salah.

## Lamulo lokhudza kukayikira pa chiwerengero cha ma Rak'aat mu Salah

Katswiri wodziwika komanso wotsogola wa Shari'ah ndi Tareeqah, 'Allamah Maulana Mufti Muhammad Amjad 'Ali A'zami رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena pa tsamba 718 la buku loyamba la masamba 1250 la Bahar-e-Shari'at losindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah, nthambi yosindikiza ya Dawat-e-Islami: Ngati munthu wopemphera Salah wakhala wokayikira za chiwerengero cha ma Rak'aat opempheredwa kwa nthawi yoyamba m'moyo wake kuchokera pamene anafika msinkhu wokhwima - mwachitsanzo, akukayikira ngati wapemphera atatu kapena anayi- ayenera kuthetsa Salah popereka Salam kapena pochita chilichonse chomwe chimathetsa Salah, kapena m'malo mwake, ayenera kumaliza Salah yake potengera kuganiza kwake kwamphanvu.

Mulimonse momwe zingakhalire, ayenera kubwereza Salah iyi kuyambira pachiyambi. Cholinga chongothetsa Salah sichokwanira. Ngati izi sizinachitike kwa nthawi yoyamba koma zinachitikapo kale, ayenera kuchita zomwe kuganiza kwake kwamphanvu kuli; ngati palibe kuganiza kwamphanvu, ayenera kuvomereza kuganiza kwa chiwerengero chochepa cha ma

Rak'aat, mwachitsanzo, ngati akukayikira ngati chiwerengero cha ma Rak'aat opempheredwa ndi atatu kapena anayi, ayenera kuwatenga ngati atatu; ngati akukayikira ngati chiwerengero cha ma Rak'aat opempheredwa ndi awiri kapena atatu, ayenera kuwatenga ngati awiri ndi ena otero. Pamenepa, ayenera kuchita Qa'dah mu Rak'at yachitatu komanso yachinayi, monga momwe Rak'at yachitatu ikhoza kukhalanso yachinayi. Pambuyo pa Qa'dah ya Rak'at yachinayi, ayenera kuchita Sajdah Sahw koma ngati akutsatira kuganiza kwamphanvu, pamakhala palibe kufunikira kwa Sajdah Sahw.

## Kunyozeka kwa Satana

Bwana wanga A'la Hadrat, mtsogoleri wa Ahl-e-Sunnah, Maulana Shah Imam Ahmad Raza Khan رحمۃ اللہ علیہ anati: Ngati pali kukayikira kulikonse kuti iye wapemphera ma Rak'aat atatu kapena anayi, ayenera kuwatenga ngati atatu, kenako apemphere Rak'at imodzi yowonjezera ndikupanga Sajdah Sahw. Ngati wapemphera ma Rak'aat asanu, zili ngati kuti ma Sujood awiriwa a Sahw adzakhala ngati Rak'at imodzi, kukwaniritsa gulu la ma Rak'aat awiri. Sipadzakhala ngakhale Rak'at imodzi yomwe ili yosavomerezeka ndi Shari'ah. M'mawu ena, zili ngati ma Sujood awiri a Sahw pamodzi ndi Rak'at imodzi [mukunena kwina, yachisanu] idzasanduka kukhala gulu losiyana la ma Rak'aat awiri a Nafl Salah. Ndipo ngati wapempheradi ma Rak'aat anayi, ma Sujood awa adzanyozetsa

ndi kunyasitsa Satana chifukwa anali iye amene anayesa kupanga Salah kukhala yosavomerezeka poyambitsa kukayikira.

*(Fatawa Razawiyyah – yotchulidwa, buku. 1, tsamba. 762)*

## Woyera ntima anakwiyitsa Satana

Woyera ntima atamaliza Salah, Satana anabwera kwa iye ndipo anati, 'Siwunapemphere bwino Salah iyi; choncho, ibwereze.' Woyera ntima anayankha, 'Sindiyibwereza. Ndapemphera Salah momwe ndingathere. Ngati muli cholakwika m'menemo, ndidzapempha chikhululuko kwa Mbuye wanga.' Satana anati, 'Usawonetse ulesi mu Salah yomwe ndi ntchito yayikulu yopembedza. Si nkhani yaying'ono. Ibwereze Salah yako.' Woyera ntima anati, 'Chilichonse chomwe chinakonzedweratu chachitika. Sindibwerezanso Salah iyi.' Satana anapitiriza kukangana, 'Ndikukulangiza kuti zikuthandize iweyo. Ndine wokufunira zabwino. Uli ndi ulemerero wapamwamba pa maso pa Allah (عَزَّوَجَلَّ) ndipo Salah ndi ntchito yayikulu yopembedza. Kapolo wochita zabwino ngati iwe sakuyenera kukhala wamakani chonchi.'

Pokhumudwitsa Satana, woyera ntima anati, 'Zilibe kanthu zomwe zingachitike, sindibwereza Salah iyi. Ponena za ulemerero wanga wapamwamba pa maso pa Mulungu, ndine wokondwa ndi ulemerero wotsika pa maso pake.' Satana anati,

'Allah (عَزَّوَجَلَّ) salandira Salah yotere.' Woyera ntima anati, 'Mbuye wanga عَزَّوَجَلَّ ndi Wachisomo kwambiri. Mwa chisomo Chake, Iye عَزَّوَجَلَّ adzalandira ntchito yanga yolakwikayi. Ndachita zomwe ndikanatha kuchita.

Kulandira kupembedza ndi ntchito ya Allah عَزَّوَجَلَّ osati yanga. Tsopano choka. Sindidzachita molingana ndi manong'onong'o ako kapena kubwereza Salah iyi.' Pomaliza, Satana atawona kulephera kwake, anachoka, ali wonyozeka ndi wochititsidwa manyazi.

Kumbukirani kuti woyera ntima anakana mwachindunji kubwereza Salah kuti anyozetse Satana, kuletsa manong'onong'o ake ndi kutseka njira zake. Zikutilimbikitsa ife konse kuchita ntchito molakwika ndi mosakwanira, kusonyeza ulesi ndi kusasamala, kugwera mumsampha woyikidwa ndi Nafs ndikukhala ndi ziyembekezo zopanda nzeru pa chisomo cha Mulungu. Si chinthu chanzeru kupemphera Salah molakwika kenako nkudzitonthoza ponena kuti, 'Allah عَزَّوَجَلَّ ndi Wachisomo ndi Wokhululuka.' *(Ashi'a-tul-Lam'aat, buku. 1, tsamba. 92)*

## Njira yapadera yokanira manong'onong'o a satana

Woyera ntima nthawi zambiri ankakhala ndi manong'onong'o a satana akuti malo omwe ankapempherera Salah anali odetsedwa. Anachotsa izi popemphera Salah mwadala pamalo omwewo pomwe anali ndi kukayikira za kudetsedwa. *(Ashi'a-tul-Lam'aat, buku. 1, tsamba. 93)*

## Ndinthu musapereke chidwi ku manong'onong'o a satana

Panali wophunzira yemwe anamaliza maphunziro ake ndikukonzekera kubwerera kudziko lake. Mphunzitsi wake wolemekezeka ananfunsa, 'Kodi umachita chani Satana akamayambitsa manong'onong'o pa nthawi ya ntchito zopembedza?' Wophunzirayo anayankha, 'Ndimawachotsa.' Mphunzitsi wolemekezeka anafunsa, 'Ngati akuyambitsanso manong'onong'o, ndiye?' Wophunzirayo anayankha, 'Ndimawachotsanso.' Mphunzitsi wolemekezeka anafunsa kachitatu, kuti 'Ngati akuyambitsanso manong'onong'o kachitatu, ndiye udzatani?' Wophunzira anayankha, 'Ndidzamuchotsanso.'

Polangiza wophunzira wake, mphunzitsi wolemekezeka anati, 'Usapereke chidwi ku manong'onong'o oyambitsidwa ndi Satana pa nthawi ya kulambira. Ngati utanganidwa ndi kupewa manong'onong'o ake, adzakupanga kukhala otanganidwa nazo. Uyenera kumuchitira ngati galu wa m'busa, osamupatsa chidwi ndikupempha chitetezo cha Allah عَزَّوَجَلَّ kwa iye ponena kuti ﴿اَعُوْذُ بِاللهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْمِ﴾.

*(Ruh-ul-Bayan, buku. 1, tsamba. 6 – ndi zosintha)*

*Namazaun mayn shaytan khalal dalta hay*

*Mujhay is kay sher say bacha Ya Ilahi*

*Kumasulira: O Wamphanvu zonse! Satana amandisokoneza pa nthawi ya Salah. Nditetezeni ku zoyipa zake.*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Manong'onong'o a satana okhudza ukhondo

Satana amayambitsanso kukayikira ndi kusatsimikizika za ukhondo kudzera m'manong'onong'o ake, ponena; mwachitsanzo, 'Ichi ndi chodetsedwa; icho ndi chodetsedwa.' Sitiyenera kupereka chidwi ku manong'onong'o ake. Tili ndi kuphweka kwakukulu kuchokera ku Shari'ah kokhudzana ndi ukhondo. Anthu ena amagwa mumsampha wa manong'onong'o a satana chifukwa alibe maphunziro achipembedzo. Kumbukirani lamulo la Shar'i kuti palibe chomwe chingapangidwe kukhala chonyansa chifukwa cha kukayikira; pokhapokha ngati chikudziwika kuti chinthu chinachake ndi chonyansa. Palibe chifukwa chodandaulira kuti chinthu chinachake chikhoza kukhala chonyansa.

## Palibe chifukwa chofufuzira zokhudza nyansi

Bwana wanga A'la Hadrat, mtsogoleri wa Ahl-e-Sunnah, Maulana Shah Imam Ahmad Raza Khan رحمۃ اللہ علیہ ananena pa tsamba 515 la buku lachinayi la Fatawa Razawiyyah kuti: Motsagana ndi Sayyiduna 'Amr Bin Aas رضی اللہ عنہ mtsogoleri wa okhulupirira, Sayyiduna 'Umar Farooq-e-A'zam رضی اللہ عنہ anadutsa pa dziwe (lomwe linkaphimba malo ochepera mlingo



www.dawateislami.net

wa mapazi 225 lili ndi madzi oyima m'menemo. Lamulo ndilakuti ngati chirombo chilichonse chamwa madzi oyima, madzi otsalawo amakhala onyansa.) Sayyiduna 'Amr Bin 'Aas رَضِیَ اللهُ عَنْهُ anafunsa mwini dziwe kuti, 'Kodi zirombo zimamwanso madzi m'dziwe lanu?' (Sayyiduna 'Umar Farooq-e-A'zam رَضِیَ اللهُ عَنْهُ) anati, 'O mwini dziwe! Musatiwuze za zimenezo.' *(Muwatta Imam Maalik, buku. 1, tsamba. 48, Raqm 47)*

## Mfundo za Madani zokhudza zotsalira za nyama

Abale achisilamu okondedwa! Kodi mwawona kuti palibe chifukwa chofunsira zokhudza nyansi? N'zotheka kuti zirombo monga agalu zimamwa madzi m'dziwe. Ngati galu aliyense wamwa madzi m'dziwe lophimba malo ochepera mlingo wa mapazi 225, madzi otsala a dziwe adzakhala onyansa. Ngakhale zili choncho, madzi otsalawa adzatengedwa kuti ndi oyera kwa amene sakudziwa ngati chirombo chilichonse chamwa madzi m'menemo kapena ayi.

Zanenedwa mu lamulo nambala 10 pa tsamba 342 la buku loyamba la masamba 1250 la Bahar-e-Shari'at losindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah, nthambi yosindikiza ya Dawat-e-Islami: Zotsalira za nkhumba, galu, mkango, nyalugwe, nkhandwe, njovu, nkhandwe ndi zirombo zina ndi zonyansa. Pano pali mfundo 8 za Madani zokhudza zotsalira za nyama. Ziwerengeni ndipo pezani phindu la moyo wapadziko lapansi ndi womwe ukubwera, اِنْ شَآءَاللّٰہ عَزَّوَجَلَّ.

1. Zotsalira za nyama zomwe nyama yake ndi Halal kudya, ndi zoyera kaya ndi zamiyendo inayi [ nyama zamiyendo inayi] kapena mbalame ndipo ziribe kanthu kuti ndi zazimuna. Nyama zimenezi ndi kuphatikizapo, mwachitsanzo, ng'ombe, ng'ombe yamphongo, njati, mbuzi, nkhunda, nkhwali ndi zina zambiri.

2. Zotsalira za nkhuku yomwe imayendayenda momasuka ndikudya zinthu zonyansa ndi Makruh. Ngati ili m'khola, ndiye zotsalira zake ndi zoyera.

3. Chimodzimodzinso, zotsalira za ng'ombe zina zomwe nthawi zambiri zimadya zinthu zonyansa ndi Makruh. Ngati ng'ombe yotere yangodya kumene chinthu chonyansa ndikuyika pakamwa pake ponyansa m'madzi oyima ophimba malo ochepera mlingo wa mapazi 225, madziwo adzakhala onyansa. (Ngati imamwa madzi poyika pakamwa pake m'madzi oyenda, pakamwa pake padzakhala poyera.) Chimodzimodzinso, ngati nyama yamphongo monga ng'ombe yamphongo kapena njati yamphongo kapena mbuzi yamphongo imanunkhiza mkodzo wa nyama zidzawo zazikazi monga momwe zimachitira nthawi zambiri, zomwe zimapangitsa pakamwa pawo kukhala ponyansa, zotsalira za nyama izi zidzakhala zonyansa pankhaniyi. pokhapokha ngati sizinazimiririke nthawi yomweyo kapena nthawi yochuluka sinadutse yomwe akuganiza kuti pakamwa pake payenera kukhala poyera. Ngati nyama iliyonse yotereyo itayika pakamwa pake m'madzi okwanira kanayi omwe



www.dawateislami.net

amaphimba dera lochepera mlingo wa masikweya mita 225, madzi atatu oyamba adzakhala onyansa pomwe lachinayi lake adzakhala woyera.

4. Zotsalira za kavalo ndi zoyera.

5. Zotsalira za nyama zokhala m'nyumba monga mphaka, mbewa kapena khoswe, njoka ndi buluzi ndi Makruh.

6. Ngati mphaka wayika pakamwa pake mumphika nthawi yomweyo atadya khoswe, mphikawo udzakhala wonyansa. Ngati mphaka wanyambita magazi pakamwa pake asanayike mumphika, mphikawo sudzakhala wonyansa pankhaniyi.

7. Ndi Makruh kupanga Wudu ndi Ghusl ndi madzi a Makruh ngakhale pali madzi oyera [osakhala a Makruh]. Komabe, ngati palibe madzi oyera, palibe vuto kupanga Wudu ndi Ghusl ndi madzi a Makruh. Chimodzimodzinso, ndi Makruh kwa munthu wolemera kudya ndi kumwa zotsalira zomwe ndi Makruh. Kwa munthu wosawuka kapena wosowa, palibe vuto kudya ndi kumwa chinthu choterocho.

8. Thukuta ndi malovu a zinyama zimene zotsalira zake ndi zonyansa, ndi zonyansanso. Ndipo thukuta ndi malovu a zinyama zimene zotsalira zake ndi zoyera, ndi zoyeranso. Chimodzimodzinso, thukuta ndi malovu a zinyama zimene zotsalira zake ndi Makruh, ndi Makruh.

*(Bahar-e-Shari'at, buku. 1, tsamba. 342-344)*

## Machiritso odabwitsa a manong'onong'o a satana kudzera mu matope

Bwana wanga A'la Hadrat, mtsogoleri wa Ahl-e-Sunnah, Imam Ahmad Raza Khan رحمۃ اللہ علیہ anafotokoza pa tsamba 771 la buku loyamba la Fatawa Razawiyyah: Mmodzi mwa akuluakulu ochita zabwino رحمھم اللہ ananena kuti: Ndinali ndi manong'onong'o a satana okhudza ukhondo. Ngati zovala zanga zadetsedwa ndi matope panjira, ndinkazichapa (pomwe lamulo ndi loti matope amatengedwa kuti ndi oyera pokhapokha wina atatsimikiza kuti ndi onyansa.) Tsiku lina, ndikupita kukapemphera Salat-ul-Fajr, zovala zanga zinadetsedwa ndi matope. Ndinkafuna kuzichapa koma ndikanatha kusemphana ndi Jama'at ngati nditazichape. Mwadzidzidzi, ndinadalitsidwa ndi chiwongoko chochokera kwa Allah عزوجل. Ndinali ndi lingaliro loti ndizigubuduze m'matope, kudetsa zovala zanga zonse, ndikulowa nawo mu Salah ndili choncho. Ndinachita zimenezo ndipo sindinakumanenso ndi manong'onong'o a satana kuyambira nthawi imeneyo.

*(Al-Hadeeqah-tun-Nadiyyah, buku. 2, tsamba. 693)*

صَلُّوْا عَلَی الْحَبِیْب　　صَلَّی اللّٰہُ عَلٰی مُحَمَّد

## Matope ndi oyera pokhapokha wina atatsimikiza kuti ndi onyansa

Abale achisilamu okondedwa! Kodi mwazindikira? Uwu ndi



www.dawateislami.net

mdalitso wa maphunziro achipembedzo. Wochita zabwino wakale ankadziwa kuti matope a panjira sangatengedwe kukhala onyansa pokhapokha atadziwika kuti matopewo ndi onyansa. Choncho, anachotsa manong'onong'o a satana modabwitsa.

Zanenedwa n'kabuku ka 'Njira Yoyeretsera Zovala' losindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah, nthambi yosindikiza ya Dawat-e-Islami: Pokhapokha ngati zikudziwika kuti matope a panjira ndi onyansa (kaya chifukwa cha nvula kapena chifukwa china chilichonse), adzatengedwa kuti ndi oyera. Choncho, ngati phazi kapena nsalu zadetsedwa ndi matope ndipo Salah yapempheredwa popanda kuzitsuka, Salah idzakhala yovomerezeka koma ndibwino kusambitsa phazi kapena nsalu yodetsedwa ndi matope.

*(Bahar-e-Shari'at, buku. 1, tsamba. 394)*

## Kodi ngodya iti ya nsalu yoti iyeretsedwe?

Ngati zovala zadetsedwa ndi chonyansa koma sizikudziwika kuti ndi gawo liti lomwe ndi lonyansa, ndiye tili ndi kuphweka kwakukulu kuchokera ku Shari'ah mu ntundu uwu wa zinthu. Zanenedwa mu Fatawa Razawiyyah kuti: Ngati ngodya iliyonse ya nsalu ndi yonyansa koma sizikudziwika kuti ndi ngodya iti yomwe ndi yonyansa, ndiye ngodya iliyonse ikhoza

kuchapidwa. Nsaluyo idzatengedwa kukhala yoyera. *(Fatawa Razawiyyah – yotchulidwa, buku. 4, tsamba. 511)*

## Kodi chidzachitike ndi chani mwana akayika dzanja lake m'madzi?

Nthawi zina, mwana amayika dzanja lake m'madzi ndipo timakhala okayika ngati madziwo tsopano ndi oyera kapena onyansa. Palibe chifukwa chokhala ndi kukayikira kulikonse pankhaniyi. Akatswiri a zamalamulo achisilamu رحمهم الله ananena kuti: Madzi omwe mwana wayika dzanja lake kapena phazi lake ndi oyera pokhapokha ngati zatsimikiziridwa kuti madziwo akhala onyansa.

*(Fatawa Razawiyyah – yotchulidwa, buku. 4, tsamba. 486)*

*Taharat kay baaray mayn shaytan akser*

*Dilata hay shak, ho karam Ya Ilahi*

*Kumasulira: Satana nthawi zambiri amayambitsa kukayikira za ukhondo. O Wamphanvu zonse! Ndipatseni chisomo!*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب      صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Manong'onong'o a satana okhudza chisudzulo

Nthawi zina, Satana amayambitsa manong'onong'o, ponena kuti: 'Kumbukira! Unalankhula mawu a chisudzulo kwa nkazi

wako!' Munthawi yotereyi, ngati muli otsimikiza kuti simunasudzule nkazi wanu ndikuti lingalirolo ndi manong'onong'o a satana, ndiye muyenera kuyankha Satana kuti: 'Ndiwe wabodza. Sindinasudzule nkazi wanga.'

Pofotokoza fanizo pankhaniyi, bwana wanga A'la Hadrat, Maulana Shah Imam Ahmad Raza Khan رحمۃ اللہ علیہ ananena kuti: Imam Abu Haazim anali mmodzi mwa oyera ntima a Tabi'een. Munthu wina anabwera kwa iye ndikunena: Satana akumayambitsa manong'onong'o mu ntima mwanga. Manong'onong'o ovuta kwambiri ndi akuti amandiwuza, 'Wam'sudzula nkazi wako.' Imam nthawi yomweyo anafunsa, 'Kodi sunasudzule nkazi wako pamaso panga?' Anayankha mosokonezeka, 'Mwa Allah عَزَّوَجَلَّ! Sindinam'sudzulepo pamaso panu.' Imam anafotokoza, 'Monga mwalumbira pamaso panga, bwanji osamuwuza Satana mwa kulumbira kuti asiye kukuvutitsani.' (M'mawu ena, ngati muli otsimikiza kuti mwalumbira, muyeneranso kunena kwa Satana polumbira, 'O wokanidwa iwe! Choka! Mwa Allah عَزَّوَجَلَّ! Sindinamusudzule nkazi wanga.' *(Fatawa Razawiyyah – yotchulidwa, buku. 1, tsamba. 785)*

*Mayri parayshaniyan waswason ki*

*Tu ker door bahr-e-Raza Ya Ilahi*

*Kumasulira: O Wamphanvu zonse! Nditetezeni ku mavuto a manong'onong'o a satana chifukwa cha Raza رحمۃ اللہ علیہ!*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب      صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

Nthawi zina, pamwambo wa phwando, anthu ena amakhala ndi manong'onong'o a satana ndi kukayikira ngati chakudyacho chaperekedwa ndi ndalama za Halal kapena Haraam. Awa ndi mawu odalitsika a Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم pankhaniyi, 'Aliyense wa inu akapita kunyumba ya m'bale wanu Msilamu ndipo akakupatsani chakudya, muyenera kudya ndipo musafunse za icho. Ngati akakupatsani chakumwa chilichonse, muyenera kuchimwa ndipo musafunse za icho.'

*(Shu'ab-ul-Iman, buku. 5, tsamba. 67, Hadees 5801)*

## Kufunsa za chakudya kungatsegule chitseko cha machimo

سُبْحٰنَ اللّٰه عَزَّوَجَلَّ!Chipembedzo chathu n'chosavuta bwanji! Ngati tikanapeza maphunziro achipembedzo! Kupeza maphunziro achipembedzo ndi njira yochotsera manong'onong'o a satana. N'zonvetsa chisoni! Nthawi zambiri timagwa nsampha wa manong'onong'o a satana chifukwa chosadziwa za chipembedzo.

Bwana wanga A'la Hadrat, Imam Ahmad Raza Khan رحمۃُ اللّٰہِ علیہ ananena pa masamba 528 ndi 529 a buku lachinayi la Fatawa Razawiyyah: Hujjat-ul-Islam kuti, woganiza kwambiri wa Ummah, Imam Abu Haamid Muhammad Bin Muhammad Bin Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena m'buku la Ihya-ul-'Uloom: Ndikunena kuti sizololedwa kwa mlendo kumufunsa

wolandira alendo ngati chakudyacho chachokera ku njira za Halal. Ngati akufuna kukhala wochita zabwino, ayenera kungopewa kudya chakudyacho modekha. Ngati kuli kofunikira kupita ku msonkhano, ayenera kudya chakudyacho popanda kufunsa za icho. Kufunsa ngati chakudyacho chaperekedwa ndi njira zovomerezeka kapena ayi kudzayambitsa mavuto ndi nkhawa ndipo kudzawulula zofowoka, zomwe mosakayikira ndi Haraam.

(Pambuyo popereka malangizo ena, Imam Ghazali رَحْمَةُ اللّٰہِ عَلَيْه ananenanso kuti) Pali anthu ambiri osadziwa omwe amakana zinthu zapadziko lapansi. Amayambitsa nkhawa ndi mavuto pofunsa za chakudya, pogwiritsa ntchito mawu owopsa. Kwenikweni, Satana amawapangitsa kuganiza kuti akuchita chinthu chabwino kwambiri pochitira anthu otere mwankhanza. Anthu amtunduwu amangofuna kukhala otchuka chifukwa chodya chakudya cha Halal chokha. Ngati akufuna kutsatira chipembedzo panthawiyi, ayenera kudziwa kuti kuopa kuwakhumudwitsa Asilamu ndi kwakukulu kuposa kuwopa kudya chinthu chokayikitsa. Ayenera kudziwa kuti sadzafunsidwa za chinthu chomwe sakudziwa; malinga ngati palibe chizindikiro chomwe chimapangitsa kukhala koyenera kupewa kudya. Choncho, kumbukirani! Kuchita za wumulungu kumafuna kuti musafunse kapena kufufuza za chakudya. Ngati kuli kofunikira kudya, mukhoza kudya ndi maganizo abwino. Uku ndi kuchita za wumulungu panthawiyi.

*(Ihya-ul-'Uloom, buku. 2, tsamba. 150)*



www.dawateislami.net

*Dil pay shaytan nay Aqa hay jamaya qabzah*

*Hoon gunahaun mayn giriftar Rasool-e-'Arabi*

*Ah! Berhta hi chala jata hay marz-e-'isyan*

*Do shifa Sayyid-e-Abrar Rasool-e-'Arabi*

*Kumasulira: O Bwana wanga (صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم)!! Satana watenga ulamuliro wa ntima wanga. Ndakodwa mu dambo la machimo. Kalanga ine! Matenda a machimo akupitirira kukula. O Mfumu ya Aneneri (صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم)! Chonde, ndichiritseni.*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Mitundu iwiri ya Satana

Zonse zomwe zatchulidwa pamwambapa zinali kufotokozera za Asatana monga m'maonekedwe a jini. Monga iwo, Asatana monga anthu amayesanso kusocheretsa anthu, kuyambitsa kukayikira ndi kusatsimikizika m'mitima. Nachi chidule cha mawu a A'la Hadrat, Imam Ahmad Raza Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه: Pali mitundu iwiri ya Asatana:

1. Asatana m'mawonekedwe a jini, mwachitsanzo, mdyerekezi wotembereredwa ndi ana ake.
2. Satana m'mawonekedwe a anthu, mwachitsanzo, osakhulupirira ndi amene amayitanira anthu ku kusakhulupirira ndi kupatuka.

Atsogoleri ndi akatswiri odziwika a Chisilamu ananena kuti, 'Vuto la Satana wawumunthu ndi lalikulu kuposa la Satana wa jini.'

*(Fatawa Razawiyyah – yotchulidwa, buku. 1, masamba 780-781)*

Mu Surah An-Naas, Allah عَزَّوَجَلَّ wapereka lamulo lopempha chitetezo kuchokera ku Asatana onsewa. Allah عَزَّوَجَلَّ wanena kuti:

الَّذِىۡ يُوَسۡوِسُ فِىۡ صُدُوۡرِ النَّاسِ ۙ﴿۵﴾ مِنَ الۡجِنَّةِ وَالنَّاسِ ﴿۶﴾

*Amene amanong'oneza m'mitima mwa anthu. Pakati pa ma jini ndi anthu.*

*[Kanz-ul-Iman (Kutanthawuzira kwa Quran)] (Gawo 30, Surah An-Naas, Vesi 5-6)*

## Asatana m'mawonekedwe a munthu

Zanenedwa mu Hadees kuti Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anamuwuza Sayyiduna Abu Zar Ghifari رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ, 'Pemphani chitetezo cha Allah عَزَّوَجَلَّ kuchokera ku zoyipa za Asatana m'mawonekedwe munthu ndi Asatana m'mawonekedwe a jini.' Sayyiduna Abu Zar Ghifari رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ anafunsa modzichepetsa, 'Kodi palinso Asatana m'mawonekedwe a anthu?' Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anayankha, 'Inde.' *(Musnad Imam Ahmad, buku. 8, tsamba. 130, Hadees 21602)*



www.dawateislami.net

Motero, onse osakhulupirira, opembedza milungu yambiri, opotoka, ampatuko ndi onyoza Mtumiki Woyera ndi Asatana m'mawonekedwe a anthu. Tiyenera kupempha chitetezo kuchokera ku zoyipa za Satana komanso a anthu awa. Koma n'zonvetsa chisoni! Asilamu ambiri amakumana nawo momasuka komanso pafupipafupi ndipo amawamvetsera mwachidwi. Anthu osadziwa amenewa amapitanso ku mapulogalamu awo otchedwa achipembedzo komanso kumawerenga zolemba zawo. Chifukwa chosadziwa za chipembedzo chawo, anthuwa amakhala ndi kukayikira, poganiza 'kodi akutsatira njira yoyenera kapena ife?' Ena amagwidwa mumsampha wawo moyipaa kwambiri moti amayimba matamando awo ndikumanena kuti, 'Zimene akunena ndizolondolanso.'

Powalangiza Asilamu kuti apewe anthu oterowo, Bwana wanga A'la Hadrat, mtsogoleri wa Ahl-e-Sunnah, Maulana Shah Imam Ahmad Raza Khan رحمۃ اللہ علیہ ananena pa masamba 781 ndi 782 a buku loyamba la Fatawa Razawiyyah kuti: O abale! Ndi chani chimene chili chothandiza kwa inu ndipo ndi chani chimene chili chopereka vuto kwa inu? Kodi mukuchidziwa kapena Allah عزوجل ndi Mtumiki Wake صلی اللہ علیہ وآلہ وسلم akuchidziwa kuposa inu? [Ndithudi, iwo akudziwa bwino.] Choncho alamula kuti Satana akabwera kudzakusocheretsani poyambitsa manong'onong'o, muyenera kumupatsa yankho lachindunji, ponena kuti, 'Ndiwe wabodza.' Musapite kwa iwo (osakhulupirira, opotoka ndi ampatuko) ndipo musawanvere

iwo chifukwa adzanyoza Mbuye wanu عَزَّوَجَلَّ, Quran Yopatulika ndi Mtumiki wanu صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم.

(Pambuyo popereka malangizo ena, A'la Hadrat رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananenanso kuti Allah عَزَّوَجَلَّ wanena mu Vesi 112 ya Surah Al-An'aam, gawo 8) kuti:

وَلَوْ شَآءَ رَبُّكَ مَا فَعَلُوْهُ فَذَرْهُمْ وَمَا يَفْتَرُوْنَ ﴿١١٢﴾

*Ndipo ngati Mbuye wanu akanafuna, sakanachita zimenezo; choncho asiyeni ndi zopeka zawo.*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 8, Al-An'aam, Vesi 112)*

Chonde ganizirani! Kodi munalamulidwa kuwasiya ndi kukana zomwe akunena kapena kupita ndikumawanvera iwo? Mu Vesi yotsatira (mwachitsanzo, Vesi 113) ya Surah Al-An'aam, Allah عَزَّوَجَلَّ wanenanso:

وَلِتَصْغٰۤى اِلَيْهِ اَفْـِٕدَةُ الَّذِيْنَ لَا يُؤْمِنُوْنَ
بِالْاٰخِرَةِ وَلِيَرْضَوْهُ وَلِيَقْتَرِفُوْا مَا هُمْ مُّقْتَرِفُوْنَ ﴿١١٣﴾

*Ndipo kotero kuti mitima ya amene samakhulupirira za dziko likubwera zipendekere ku zopeka zawo ndipo kuti iwo azikonda zopeka zimenezo, ndipo achite machimo omwewo amene iwo akuwachita.*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 8, Al-An'aam, Vesi 113)*

Onani! Kubwereketsa khutu ku zomwe iwo amanena kunalengezedwa kukhala mchitidwe wa amene sakhulupirira za moyo umene ukubwera. Zotsatira zake, zinthu zotemberereredwa zomwe iwo amanena zikhoza kukhala ndi zotsatira pa mitima ya onvera omwe angakhalenso ngati iwo. ﴿وَالْعِيَاذُ بِاللّٰهِ تَعَالٰى﴾ tikupempha chitetezo cha Allah عَزَّوَجَلَّ ku zimenezi). Anthu amaganiza mosadziwa kuti sitidzakopeka ndi iwo chifukwa ndife Asilamu enieni. Anthu awa ayenera kunvetsera mwachidwi mawu otsatirawa a Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم: 'Aliyense amene wanva nkhani ya [kuwonekera kwa] Dajjaal ayenera kuthawa kuchokera kwa iye. Ndikulumbira mwa Allah عَزَّوَجَلَّ! Munthu adzapita kwa iye ndipo adzaganiza kuti ndine Msilamu ndipo sindidzapatsidwa vuto ndi iye koma iye [munthuyo] adzanyengedwa ndi iye [Dajjaal], kukhala wotsatira wake.'

*(Sunan Abi Dawood, buku. 4, tsamba. 157, Hadees 4319)*

Kodi muli ndi maganizo akuti padzakhala Dajjaal mmodzi yekha, wonyansa kwambiri, amene adzabwera pambuyo pake? Ayi! Onse amene amayitanira ku kupatuka ndi a Dajjaal ndipo ndi koyenera kuthawa kwa onsewo. Chiwopsezo chomwecho chomwe chatchulidwa pamwambapa chili mu kukumana nawo ndi kuwanvetsera. Mtumiki Wamkulu ndi Wolemekezeka Kwambiri صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ananena kuti, 'M'nthawi yomaliza, padzakhala anthu a Dajjaal omwe adzakhala abodza. Adzakuwuzani zinthu zotere zomwe simunazinvepo inu kapena

makolo anu. Choncho khalani kutali nawo ndipo asungeni kutali ndi inu kuti asakusocheretseni ndikukuponyani inu m'chisokonezo.' *(Sahih Muslim, tsamba. 9, Hadees 7; Fatawa Razawiyyah – zatchulidwa, buku. 1, tsamba. 781-782)*

*Sarwar-e-Deen! Li-jiye apnay natuwano" ki khabar*

*Nafs-o-Shaytan Sayyida! Kab tak dabatay jayain gey*

*Kumasulira: O Mfumu ya chipembedzo (صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم)! Chonde samalirani akapolo anu ofowoka. Kodi Nafs ndi Satana adzapitiriza kutipondereza mpaka liti?*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب     صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## MACHIRITSO A MANONG'ONONG'O A SATANA

### Satana m'mawonekedwe a chule

Sayyiduna 'Umar Bin 'Abdul 'Azeez رضی اللّٰه عنہ ananena kuti munthu wina anapemphera kwa Allah عَزَّوَجَلَّ m'mawu awa, 'O Allah عَزَّوَجَلَّ! Chonde ndiwonetseni momwe Satana amayambitsira manong'onong'o mu ntima mwa anthu.' Munthuyo analota kuti pali munthu ali ndi thupi lowonekera. Pakati pa phewa ndi khutu la munthuyo, Satana m'mawonekedwe a chule anali atakhala ndikumayambitsa manong'onong'o polowetsa thunthu lake lalitali ndi lopyapyala kuchokera pa phewa kupita ku ntima wa munthuyo. Nthawi

iliyonse munthuyo akakumbukira Allah عَزَّوَجَلَّ, Satana amachoka. *(Mukashafa-tul-Quloob, tsamba. 59)*

## Mtumiki Woyera nthawi zonse ankamukumbukira Allah عَزَّوَجَلَّ

Abale achisilamu okondedwa! Izi zikusonyeza kuti kumukumbukira Allah عَزَّوَجَلَّ ndi machiritso othandiza a manong'onong'o a satana chifukwa Satana amathamangitsidwa ndi kumukumbukira Allah عَزَّوَجَلَّ. Mtumiki wathu Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankakhala mphindi iliyonse ndikupuma mpweya uliwonse akumukumbukira Allah عَزَّوَجَلَّ. Pamene pali kuthekera, tiyenera kupitiriza kunena 'Allah, Allah' kapena kuwerenga Salat-'Alan-Nabi m'malo mokhala chete mosafunikira. Mwanjira imeneyi, tidzapitiriza kupeza mphoto ndipo Satana nayenso adzafowoka kwambiri, اِنْ شَآءَاللّٰه عَزَّوَجَلَّ. *(Ihya-ul-'Uloom, buku. 3, tsamba. 37)*

## Satana – wofowoka ngati mpheta

Hujjat-ul-Islam, Sayyiduna Imam Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena kuti: Sayyiduna Qays Bin Hajjaj رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati: Satana wanga oyenda naye anandiwuza kuti, 'Nditangolowa m'thupi lako ndinali (Wamphanvu) ngati ngamira koma tsopano ndakhala (wofowoka) ngati mpheta.' Sayyiduna Qays Bin Hajjaj رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anafunsa, 'Chifukwa chani?' Satana anayankha, 'Umapitiriza kundisungunula [kundifowoketsa]

pomukumbukira Allah عَزَّوَجَلَّ.' *(Ihya-ul-'Uloom, buku. 3, tsamba. 37)* Motero, kunyalanyaza kumukumbukira Mulungu si chinthu chabwino.

## Satana amachoka

Sayyiduna Ibn 'Abbas رضی اللہ عنہما ananena kuti, 'Satana amapitiriza kukhala pa ntima pa kapolo. Kapolo akanyalanyaza kumukumbukira Mulungu, Satana amayambitsa manong'onong'o ndipo kapolo akamukumbukira Allah عَزَّوَجَلَّ, Satana amachoka.'

*(Musannaf Ibn Abi Shaybah, buku. 9, tsamba. 392)*

## Nkhondo pakati pa Zikr ndi manong'onong'o a satana

Hujjat-ul-Islam, Sayyiduna Imam Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati: Pothirira ndemanga pa Mawu a Mulungu otsatirawa:

مِنْ شَرِّ الْوَسْوَاسِ ۙ۬ الْخَنَّاسِ ۪ۙ ﴿۴﴾

*Ku zoyipa za amene amayambitsa maganizo oyipa a m'mitima ndipo amabisala.*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 30, Surah An-Naas, Vesi 4)*

Sayyiduna Mujahid رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena kuti: Satana wadziyika pa ntima pa munthu. Munthu akamukumbukira Allah عَزَّوَجَلَّ, Satana amabwerera ndipo akanyalanyaza, Satana amadziyika pa ntima.



www.dawateislami.net

Nkhondo pakati pa Zikr ndi manong'onong'o a satana imapitirira; monga 'nkhondo' pakati pa usana ndi usiku ndi pakati pa kuwala ndi mdima imapitirira. Ziwirizi, kumukumbukira Mulungu komanso manong'onong'o a satana – ndi zotsutsana. Allah عَزَّوَجَلَّ wanena mu Vesi 19 ya Surah Al-Mujadalah, gawo 28:

اِسۡتَحۡوَذَ عَلَیۡہِمُ الشَّیۡطٰنُ فَاَنۡسٰہُمۡ ذِکۡرَ اللّٰہِ ؕ

*Mdyerekezi anawalamulira ndipo anawapangitsa kuyiwala kumukumbukira Allah.*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 28, Al-Mujadalah, Vesi 19)*

## Satana amadya ntima

Sayyiduna Anas رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُ anafotokoza kuti Mtumiki Wokondedwa ndi Wodalitsika صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati, 'Satana amayika thunthu lake pa ntima pa munthu. Ngati munthu wamukumbukira Allah عَزَّوَجَلَّ, Satana amabwerera ndipo ngati munthu wamuyiwala Allah عَزَّوَجَلَّ, ndiye Satana amadya [amalamulira] ntima wake.' *(Abu Ya'la, buku. 3, tsamba. 453, Hadees 4285)*

صَلُّوۡا عَلَی الۡحَبِیۡب صَلَّی اللّٰہُ عَلٰی مُحَمَّد

## Kusalapa ngakhale mutakwanitsa zaka 40

Zanenedwa kuti: Munthu akafika zaka 40 ndipo samalapa machimo, Satana amasisita nkhope ya munthu wotere, ponena,

'Ndikhoza kuperekedwa nsembe pa nkhope iyi yomwe sidzapeza chipulumutso.' *(Ihya-ul-'Uloom, buku. 3, tsamba. 35)*

Mwana wokondedwa wa A'la Hadrat, Wolemekezeka Mufti-e-A'zam Hind wapempha kwa Allah عَزَّوَجَلَّ mu vesi zotsatirazi:

*Jo hay ghaafil Tayray zikr say Zul-Jalal*

*Us ki ghaflat hay us per wabaal-o-nakaal*

*Qa'r-e-ghaflat say ham ko Khudaya nikaal*

*Ham haun zaakir Tayray aur mazkoor Tu*

﴾اَللّٰہُ اَللّٰہُ اَللّٰہُ اَللّٰہُ﴿

*Kumasulira: O Wamphanvu zonse! Kunyalanyaza kukukumbukirani inu ndi vuto komanso chilango kwa munthu wonyalanyaza. O Wamphanvu zonse! Titulutseni m'dzenje la kunyalanyaza ndipo tidalitseni ndi kukukumbukirani inu.*

*(Saaman-e-Bakhshish)*

صَلُّوْا عَلَی الْحَبِیْب صَلَّی اللّٰہُ عَلٰی مُحَمَّد

## Musapereke chidwi ku manong'onong'o a satana

Abale wokondedwa achisilamu! amodzi mwa machiritso a manong'onong'o a satana ndi akuti sitiyenera kuwapatsa chidwi konse. Tikangonva manong'onong'o a satana, ngati tingayambe kuganiza za zigwa zokongola za Makkah Mukarramah,



www.dawateislami.net

kuyendera modzichepetsa Masjid-ul-Haraam ndi kupsopsona Hajar-e-Aswad mobwerezabwereza ndikuzungulira Ka'bah yodalitsika mwachidwi m'maganizo! Ngati tingatayike m'zikumbukiro ndi zochitika zokongola za Madinah! Ngati nthawi zina tingaganize za minga zokongola za Madinah ndipo nthawi zina za maluwa ake okopa maso; nthawi zina za zigwa zokongola za Madinah ndipo nthawi zina za misewu yowala ya Madinah; nthawi zina za mapiri odabwitsa a Madinah ndipo nthawi zina za zipululu zokongola za Madinah!

Ngati tinakasangalala nthawi zina poganizira za mlengalenga woyera wa Madinah ndipo nthawi zina za mphepo zonunkhira za Madinah; nthawi zina za mawonekedwe okongola a Mphika Wobiriwira ndipo nthawi zina za kukhala mwa ulemu pamaso pa Geti la Golide! Ngati chidwi chanu chikukulimbikitsani, ndiye ganizirani za Mtumiki Wankulu ndi Wolemekezeka Kwambiri صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Ngati tingadalitsidwe ndi chisoni chachikulu, chikondi, chidwi ndi kudzipereka kwa Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم moti mpakana timasulidwe ku chisoni chilichonse cha dziko lapansi komanso ku manong'onong'o a satana. Ngati pemphero lotsatirali likanayankhidwa kwa ife!

*Aysa guma day un ki wila mayn Khuda hamayn*

*Dhoonda karayn per apni khabar ko khabar na ho*

*Kumasulira: Allah* عَزَّوَجَلَّ *atipatse kudzipereka kwakukulu kwa Mtumiki Woyera* صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم *koti sitingathe "kudzipeza" tokha*

*ngakhale titakhala "tikufufuza", mukunena kwina, tikhale munkhalidwe lopambanitsa ndi wapamwamba mu kudzipereka kwake! (Hadaiq-e-Bakhshish)*

اٰمِیْن بِجَاہِ خَاتَمِ النَّبِیّٖن صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم

## Machiritso 8 a manong'onong'o a satana

1. Pemphani thandizo kwa Allah عَزَّوَجَلَّ kuti mukhale otetezeka kwa Satana. Nthawi iliyonse mukakumana ndi manong'onong'o a satana, yambani kumukumbukira Allah عَزَّوَجَلَّ.
2. Nenani ﴿اَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْمِ﴾.
3. Nenani ﴿لَا حَوْلَ وَلَا قُوَّةَ اِلَّا بِاللّٰهِ﴾.
4. Werengani ﴿سُوْرَةُ النَّاس﴾ [Surah An-Naas].
5. Nenani ﴿اٰمَنْتُ بِاللّٰهِ وَرَسُوْلِهٖ﴾
6. Werengani Vesi yodalitsika yotsatirayi, manong'onong'o a satana adzathetsedwa nthawi yomweyo:

هُوَ الْاَوَّلُ وَ الْاٰخِرُ وَ الظَّاهِرُ وَ الْبَاطِنُ ۚ وَ هُوَ بِكُلِّ شَیْءٍ عَلِیْمٌ ﴿۳﴾

*(Gawo 27, Surah Al-Hadeed, Vesi 3)*

7. Werengani Du'a yotsatirayi mochuluka kumachotsa manong'onong'o a satana:

سُبْحٰنَ الْمَلِكِ الْخَلَّاقِ ﴿اِنْ يَّشَاْ يُذْهِبْكُمْ وَيَاْتِ بِخَلْقٍ جَدِيْدٍ ﴿۱۹﴾ وَّمَا ذٰلِكَ عَلَى اللّٰهِ بِعَزِيْزٍ ﴿۲۰﴾﴾

*(Gawo 13, Surah Ibraheem, Vesi 19, 20)*

*(Chidule chochokera mu: Fatawa Razawiyyah – chatchulidwa, buku. 1, tsamba. 770)*

*(Gawo la Vesi yomwe ili mu Du'a yomwe ili pamwambapa layikidwa mu m'mikutira mawu pa ndi mtundu wina wa zilembo.)*

8. Wothirira ndemanga wodziwika, woganiza kwambiri wa Ummah, Mufti Ahmad Yar Khan رَحۡمَةُاللّٰهِعَلَيۡه ananena kuti: Masufi odalitsika رَحِمَهُمُ اللّٰه ananena kuti: Aliyense amene amawerenga ﴿لَا حَوْلَ وَلَا قُوَّةَ اِلَّا بِاللّٰهِ الْعَلِيِّ الْعَظِيْمِ﴾ kokwana ka 21 m'mawa ndi madzulo uliwonse, n'kuwuzira m'madzi ndikumwa, adzakhalabe otetezeka ku manong'onong'o a satana kwambiri اِنۡ شَآءَاللّٰه عَزَّوَجَلَّ

*(Mirat-ul-Manajih, buku. 1, tsamba. 87)*

*Muheet dil pay huwa haye Nafs-e-ammarah*

*Dimagh per mayray Iblees chha gaya Ya Rab*

*Riha`ee mujh ko milay kash! Nafs-o-shaytan say*

*Tayray Habib ka dayta hoon wasitah Ya Rab*



www.dawateislami.net

*Kumasulira: Nafs yanga yoyipa yatenga ulamuliro wa ntima wanga ndipo Satana walamulira maganizo anga. O Wamphanvu zonse! Ndimasulidwe ku Nafs ndi Satana chifukwa cha Mtumiki Wanu Wokondedwa* صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم*!*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Zoyenera kuchita ngati manong'onong'o a satana sakutha?

Ngati munthu sanathe kuchotsa manong'onong'o a satana ngakhale powerenga mapemphero ndi kuchita ntchito zina, palibe chifukwa chodandawulira. Pano pali chidule cha zomwe Hujjat-ul-Islam, Sayyiduna Imam Muhammad Ghazali رحمۃ اللّٰہِ علیہ ananena m'buku lake la Minhaj-ul-'Aabideen losindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madinah, nthambi yosindikiza ya Dawat-e-Islami: Ngati mukuwona kuti Satana sakusiya kukuvutitsani ndipo akuyesera kukulamulirani ngakhale kuti mwapempha chitetezo cha Allah عَزَّوَجَلَّ kuchokera kwa Satana, zikutanthawuza kuti Allah عَزَّوَجَلَّ akufuna akuyeseni khama lanu, mphanvu zanu ndi kuleza ntima kwanu. Ndiye kuti, Allah عَزَّوَجَلَّ akukuyesani ngati mungalimbane ndi Satana kapena kulephera nkhondo yolimbana naye.

Onani! Allah عَزَّوَجَلَّ wapereka ulamuliro kwa osakhulupirira ndi ena ambiri pa ife, pamene Iye عَزَّوَجَلَّ ndi Wamphanvu zonse ndipo akhoza kuthetsa chisokonezo ndi zoyipa zomwe



www.dawateislami.net

zimayambitsidwa ndi iwo ngakhale popanda ife kuchita Jihad koma Iye عَزَّوَجَلَّ sachita zimenezo. M'malo mwake, Iye عَزَّوَجَلَّ amalamula akapolo kuchita Jihad kuti Iye عَزَّوَجَلَّ ayese kuti ndani ali wachidwi ndi wofunitsitsa za Jihad ndi kuphedwa ndipo ndani amene amalimbana nawo mowona ntima ndi moleza ntima.

Pambuyo popereka malangizo ena, Sayyiduna Imam Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena kuti: Choncho ifenso talamulidwa kukhala tcheru ndi okangalika pa nkhondo yolimbana ndi Satana. Akatswiri athu a Chisilamu ananenanso kuti: Kuti mulimbane ndi Satana ndi kumulamulira, zinthu zitatu ndizofunikira:

1. Muyenera kudziwa njira zake zachinyengo ndi machenjerero ake ndikuzizindikira. Mukangodziwa, Satana sadzatha kukupatsani vuto. Ngati wakuba wadziwa kuti mwini nyumba ali tcheru ndi umbava, amathawa.

2. Musalandire konse kuyitana kosokoneza ndi kochimwa kwa Satana. Pasakhale zotsatira za kuyitana kwake pa ntima wanu. Musakonzekerenso kulimbana naye chifukwa Satana ali ngati galu wokuwa. Mukalimbana naye, adzakuwa kwambiri. Mukawanyalanyaza manong'onong'o ake, adzakhala chete.

3. Mukumbukireni Wamphanvu zonse mochuluka.

*(Minhaj-ul-'Aabideen, tsamba. 46)*



www.dawateislami.net

## Kumukumbukira Mulungu kumamupweteka Satana

Zanenedwa kuti kumukumbukira Mulungu ndi kopweteka kwambiri kwa Satana monga momwe matenda owopsa amamupwetekera munthu momwe mnofu umachoka m'thupi.

*(Minhaj-ul-'Aabideen (Chiarabu), tsamba. 46)*

*Imtihan kay kahan qaabil hoon mayn piyaray Allah*

*Bay-sabab bakhsh day Maula Tayra kya jata hay*

*Kumasulira: O Allah عَزَّوَجَلَّ! Sindingathe kuyesedwa. Ndikhululukireni popanda chifukwa. Kutikhululukira si kovuta kwa Inu konse.*

*(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 72)*

اٰمِيۡن بِجَاهِ خَاتَمِ النَّبِيّٖن صَلَّى اللهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

صَلُّوۡا عَلَى الۡحَبِيۡب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

Manong'onong'o a satana: Nthawi zambiri, manong'onong'o a satana sathetsedwa ngakhale pomukumbukira Allah عَزَّوَجَلَّ. Mwachitsanzo, Salah ndi ntundu wa ukulu kwambiri wa kumukumbukira Mulungu koma Satana amayambitsa manong'onong'o ambiri pa nthawi ya Salah. Amatipangitsa ife kukumbukira zinthu zoyiwalika pa nthawi ya Salah.

Machiritso a manong'onong'o a satana: Mosakayikira, kumukumbukira Mulungu kumathamangitsa Satana.



www.dawateislami.net

Muyenera kuti munanva kuti mapemphero amayankhidwa ndi Allah عَزَّوَجَلَّ. Palibe kukayikira zazimenezo. Zanenedwa mu Vesi nambala 60 ya Surah Al-Mu'min:

اُدْعُوْنِیْۤ اَسْتَجِبْ لَكُمْ ؕ

*Ndipempheni Ine, Ndipo ndidzakuyankhani.*

[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 24, Al-Mu'min, Vesi 60)

Komabe, zotsatira za pemphero kuyankhidwa sizimawoneka nthawi zambiri. Kwenikweni, pali malamulo ena othamangitsira Satana kudzera mu njira yomukumbukira Mulungu komanso a kuyankhidwa kwa mapemphero. Titha kutenga chitsanzo cha machiritso. Ngati zinthu zowononga sizikupewedwa, machiritso amalephera kugwira ntchito yofunikira. Ngati wodwala matenda a shuga apitiriza kudya maswiti, kodi machiritso adzakhala ndi zotsatira zotani? Chimodzimodzinso, kuti muchotse manong'onong'o a satana ndi kumuthamangitsa, kupewa machimo ndikofunikira. Ngati Umulungu siwunatengedwe kapena kuchita ntchito zabwino sikunatengedwe, ndiye machiritso monga Zikr sangachiritse matenda a manong'onong'o a satana.

Hujjat-ul-Islam, Sayyiduna Imam Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena kuti: Satana ali ngati galu wanjala amene amabwera kwa inu. Ngati mulibe nkate ndi nyama, adzachoka mosavuta mutamuwopseza. Ngati muli ndi nyama ndipo iye ali ndi njala, adzagwera pa nyama ndipo sadzathamangitsidwa mophweka.



www.dawateislami.net

Chimodzimodzinso, ngati mulibe chilichonse cha Satana muntima, amachoka muntimamo pamene kumukumbukira Mulungu kwachitika. Komano, ngati ntima uli pansi pa ulamuliro wa zilakolako, mkhalidwe wankati wa ntima udzagwidwa ndi Satana amene adzaletsa munthu wotero kumukumbukira Mulungu ndi ntima wake wonse. Kunena za ntima wa munthu ochita zabwino, siwumakhudzidwa ndi zilakolako za Nafs ndi makhalidwe oyipa a Satana samabwera kwa iwo chifukwa cha zilakolako koma amabwera pamene ntima wawo ulibe kumukumbukira Mulungu chifukwa cha kunyalanyaza. Akamukumbukira Mulungu, Satana amachoka.

*(Chidule chochokera mu: Ihya-ul-'Uloom, buku. 3, tsamba. 45)*

Mwachidule, amene amachita machimo usana ndi usiku ali ngati bwenzi la Satana. Ndipo n'zotheka bwanji kuti Satana athawe kwa abwenzi ake mosavuta! Mu Vesi 4 ya Surah Al-Hajj, Allah عَزَّوَجَلَّ anati mu gawo 17 la Quran Yopatulika:

كُتِبَ عَلَيۡهِ اَنَّهٗ مَنۡ تَوَلَّاهُ فَاَنَّهٗ يُضِلُّهٗ وَ يَهۡدِيۡهِ اِلٰى عَذَابِ السَّعِيۡرِ ﴿۴﴾

*(Mdyerekezi) amene analembedwa kuti aliyense amene angamupange kukhala bwenzi, ndithudi adzamusocheretsa ndikumutsogolera ku njira ya chilango cha Gehena.*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 17, Surah Al-Hajj, Vesi 4)*

Hujjat-ul-Islam, Sayyiduna Imam Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena kuti: Mphanvu yeniyeni ya Zikr ya Mulungu imatha kukhazikika muntima pamene wayeretsedwa ku makhalidwe



www.dawateislami.net

oyipa ndikukongoletsedwa ndi kupembedza (kuchita ntchito zabwino). Kupanda kutero, Zikr idzakhala yakanthawi ndipo singakhudze ntima kapena kuwulamulira. Zitha kuchotsanso mphanvu ya satana.

Imam Ghazali ananenanso kuti: Ngati mukufuna kukhala otetezeka kwa Satana, khalani ochita zabwino ndi odziletsa ndipo yesani machiritso monga Zikr za Mulungu. Mwanjira imeneyi, Satana adzathawa kwa inu. *(Ihya-ul-'Uloom, buku. 3, tsamba. 45, 47)*

*Nafs-o-shaytan ho gaye ghalib*

*In kay chungal say Tu chhura Ya Rab*

*Ker kay taubah mayn phir gunahaun mayn*

*Ho hi jata hoon mubtala Ya Rab*

*Neem-jan ker diya gunahaun nay*

*Marz-e-'isyan say day shifa Ya Rab*

*Kumasulira: Nafs komanso Satana andilamulira. O Wamphanvu zonse! Ndimasuleni ku ukapolo wawo. Ndimachita machimo ngakhale nditalapa. Machimo andiyandikitsa ku chiwonongeko. O Wamphanvu zonse! Ndichiritseni ku matenda a machimo.*

اٰمِیْن بِجَاہِ خَاتَمِ النَّبِیّٖن صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم

صَلُّوْا عَلَی الْحَبِیْب     صَلَّی اللّٰہُ عَلٰی مُحَمَّد



www.dawateislami.net

## Mfundo za Madani

Tikanakhala ndi chidwi mu ntchito zabwino m'malo mwa chuma ndiponso kuziwerengera pemphero zimenezi!

**Muhammad Ilyas Attar Qadiri**
16 Muharram-ul-Haraam, 1432 AH

## Maganizo a kusakhulupirira m'maganizo

Funso: Kodi lamulo la munthu amene amanena kuti maganizo a kusakhulupirira amabwera m'maganizo mwake pamene ali pamavuto ndi lotani?

Yankho: Ngati maganizo a kusakhulupirira abwera m'maganizo mwa munthu ndipo amawona kuti ndi oyipa kuwafotokoza, ndi chizindikiro cha chikhulupiriro chenicheni. Maganizo a kusakhulupirira amayambitsidwa ndi Satana wotembereredwa amene akufuna kuwononga chikhulupiriro cha Msilamu. Omutsatira Mtumiki ena odalitsika رضی اللہ عنہم anabwera pa maso pa Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndipo ananena modzichepetsa kuti, 'Tili ndi maganizo otere omwe timawona kuti ndi oyipa kwambiri kuwafotokoza.' Mtumiki Wankulu صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Kodi ndizowonadi?' Iwo ananena modzichepetsa, 'Inde.' Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Ndi chizindikiro cha chikhulupiriro choyera.' (Sahih Muslim, tsamba. 80, Hadees 132) Katswiri wodziwika komanso wotsogola wa Shari'ah ndi Tareeqah, 'Allamah Maulana Mufti Muhammad Amjad Ali



www.dawateislami.net

Azami رحمۃ اللہ علیہ ananena kuti: Ngati lingaliro la kusakhulupirira labwera mu ntima mwa munthu ndipo amaliwona kuti ndi loyipa kulifotokoza m'mawu, ndiye si kusakhulupirira koma ndi chizindikiro chapadera cha chikhulupiriro. Kodi akanalitenga kuti ndi loyipa, akanakhala kuti alibe chikhulupiriro mu ntima mwake! *(Bahar-e-Shari'at, buku. 2, gawo 9, tsamba. 456)*

Funso: Ngati wina wafotokoza kwa munthu wina kuti, 'Ine ndimakumana ndi manong'onong'o a satana onyozetsa otere. Ndatopa nawo. Chonde ndi uzeni machiritso aliwonse.' Kodi adzayimbidwa mlandu wa kusakhulupirira pankhaniyi?

Yankho: Ayi, sadzayimbidwa mlandu wa kusakhulupirira pankhaniyi.

*(Kufriyah Kalimat kay baaray mayn Suwal jawab, tsamba. 423-424)*



www.dawateislami.net

الحمد لله رب العلمين والصلوة والسلام على سيد المرسلين اما بعد فاعوذ بالله من الشيطن الرجيم بسم الله الرحمن الرحيم

## KUTI MUKHALE MSILAMU WOPEMBEDZA KOMANSO WOSWALI

Khalani usiku wonse ku nsonkhano wolimbikitsa Sunnah (Ijtima) wa Dawat-e-Islami womwe umachitika Lachinayi lililonse pambuyo pa Swala ya Maghrib mu nzinda wanu, kufuna kukondweretsa Allah ndi cholinga chabwino (Niya).

Kuti muphunzire ma Sunnah, pangani kukhala chizolowezi chanu kuyenda ndi Madani Qafilah ya masiku atatu (3) mwezi uliwonse pamodzi ndi okonda Mtumiki, kulemba nkabukunse ka Madani In'amat tsiku lilionse pochita Fikr-e-Madina, ndipo muzikapereka kwa m'bale wachisilamu woyang'anira (Zimmedar) wa n'dera lanu pa tsiku loyamba la mwezi uliwonse wa Madani.

**Cholinga changa cha Madani:** Ndiyenera kuyesetsa kudzikonza ndekha ndi anthu a dziko lonse lapansi. Kuti tidzikonze tokha, tiyenera kutsatira Madani In'amat, ndipo kuti tiyesetse kukonza anthu a dziko lonse lapansi, tiyenera kuyenda ndi Madani Qafilah.

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah, Mahallah Saudagaran
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan
UAN: +92 21 111 25 26 92 | Ext: 7213
Web: www.dawateislami.net | E-mail: translation@dawateislami.net